KHULĀSAH NŪR AL-YAQĪN MCHICHEWA

Lolembedwa ndi:

Umar Abd al-Jabbār (r.a)

Ndipo latanthauziridwa mchichewa ndi:

Zaid Bunāya Abū Muhammad

(Allah amuyang'anire nthawi zonse, Amin)

MAU OYAMBA

Mdzina la Allah Wachifundo chambiri, Wachisoni chosatha

Kutamandidwa konse ndi kwa Allah amene watsogolera akapolo ake kupyolera mu nkhani za (anthu) omwe adapita (kale), ndikuzipanga kukhala phunziro kwa otsatira pambuyo kufikira tsiku lachiweruzo. Ndipo madalitso ndi mtendere ukhale kwa bwana wathu Muhammad (s.a.w) amene moyo wake unali odzadzidwa ndi makhalidwe apamwamba ndi mbiri zabwino. (Madalitso ndi mtendere ukhalenso) pa akubanja ake ndi ophunzira ake amene anachita mbiri ya Mtumikiyi kukhala nyali yofalitsira chipembedzo, mpakana adakafika ku chipupa (cha mpanda) wa dziko la China kummawa, ndi ku mkatikati mwa maiko a ku Ulaya kumadzulo.

Pambuyo pake;

Pamene mbiri ya Mtumiki (s.a.w) ili chokonzera chachikulu cha mitima yopotoka komanso sukulu yayikulu zedi yomwe imadzala mmitima kukula kwa chikhulupiriro, komanso dangalira lake langwiro, komanso chifuniro champhamvu ndi kugwiritsitsa choonadi, ndi kudzikongoletsa ndi makhalidwe abwino, ndi mbiri zapamwamba, (chifukwa cha zonsezi) ndidaona kuti ndiwafupikitsire ndi kuwalembera mwachidule ophunzira a masukulu (achisilamu) oyamba kumene (primary), ma phunziro (lessons) ochokera mmbiri yake (s.a.w), pogwiritsira ntchito chiyankhulo chosavuta kwa mphunzitsi pamene akuphunzitsa, komanso kwa ophunzira kuwamvetsetsa (maphunzirowa) ndi kuwerenga.

Ndipo ndidasankha – pakati pa mabuku a mbiri ya chisilamu – buku la **Nūrul-Yaqīn Fī Sīrati-Sayydil-Mursalīn**, kutanthauza (Kuwunika kwa chikhulupiriro pa mbiri ya Bwana wa Atumiki). Buku lolembedwa ndi Marhum (malemu) Al-Khudarī Bik (Allah awachitire chisoni). Chifukwa cha kudalira kwawo pa Qur'ān ndi Hadīth pa kufotokoza kwawo, komanso chifukwa cha kudziwika kwake (bukuli) pakati pa anthu wamba ndi anthu osankhika.

Ndipo ndayika pambuyo pa phunziro lililonse, ndime yapadera yofotokoza chidule cha nkhani yonse. Chomwecho ndikumupempha Allah kuti ayichite (ntchitoyi) kukhala yolandirika komanso yongofuna chiyanjo chake basi. Ndithu Iye pachimene wafuna Ndiwakutha, ndipo pa kuyankha pempho ali Oyenerera.

`Umar `Abdul-Jabbār

بِسْمِ اللهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيْمِ

Mbiri ya Bwana wathu Muhammad

Madalitso ndi mtendere ukhale pa Iye

Sitili osawukira (kuwerenga) mbiri ya moyo wa anthu anzeru a chigiriki ndi aluntha a ku Romu, ndi ophunzira a chifaransa, pakuti tili nawo mu mbiri yathu moyo olemekezeka odzadzidwa ndi khama ndi ntchito, ndi kupirira ndi kulimba mtima, ndi chikondi ndi chisoni, ndi luntha ndi kayendetsedwe ka dziko, ndi ulemelero weni-weni, ndi umunthu okwanira. Ndipo umenewu ndi; Moyo wa Mtumiki wathu (s.a.w), ndipo watikwanira (kukhala chitsanzo).

Mus̲tafa Lutfi Al-Manfulu̲ti

GAWO LOYAMBA

Kuchokera mmoyo wa Mtumiki wa Allah (s.a.w)

(1) BWANA WATHU MUHAMMAD (S.A.W)

1) Iye ndi otumizidwa wa Allah kwa anthu onse komanso otsiriza wa Aneneri ndi mtsogeleri wa Atumiki (a.s).

2) Iye adadza ndi chipembedzo cha Chisilamu, chomwe Allah sakalandira chipembedzo china tsiku la chiweruzo koma icho basi.

3) Ndipo Iye ndi ochokera mwa anthu olemekezeka achiquraysh, mtundu olemekezeka zedi pa mzinda wa Makkah olemekezeka.

4) Ndipo mndandanda wa makolo ake umalumikizana ndi Isma`īl mwana wa Ibrāhīm (mtendere wa Allah ukhale pa awiriwo).

MAFUNSO

Kodi bwana wathu Muhammad (s.a.w) ndi ndani? Adadza ndi chiani? Kodi makolo ake awiri ndi ochokera mu fuko lanji? Mndandanda wa makolo ake umalumikizana ndi ndani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Bwana wathu Muhammad (s.a.w): Iye ndi otumizidwa wa Allah kwa anthu onse. Adadza ndi chipembedzo cha Chisilamu. Ndipo Iye ndi wachiarabu, wachiquraysh, ochokera mwa `Adnān.

(2) MNDANDANDA WA MAKOLO AKE NDI KUMWALIRA KWA ATATE AKE

1) Bambo ake ndi: `Abdullāh mwana wa `Abdul-Muttalib, mwana wa Hāshim, mwana wa `Abd-Manāf, mwana wa Qusayy, mwana wa Kilāb.

2) Mai ake ndi: Āminah mwana wa Wahab, mwana wa Abd-Manāf, mwana wa Zuhrah, mwana wa Kilāb.

3) Chomwecho mai ake akukumanizana ndi atate ake pa agogo ake a chisanu omwe ndi Kilāb.

4) Ndipo ndithu bambo ake adamwalira iye akadali mmimba mwa mai ake, zaka zawo zili khumi ndi zisanu ndi zitatu (18), ndipo adayikidwa ku Madinah. Ndipo Iwo sadamusiyire Iye chilichonse chochokera mchuma.

MAFUNSO

Kodi mndandanda wa makolo ake kumbali ya bambo ake ndi uti? Nanga mndandanda wa makolo ake kumbali ya mai ake ndi uti? Kodi mai ake amalumikizana ndi atate ake pa agogo ake ati? Kodi atate ake adamwalira nthawi liti? Nanga anayikidwa kuti?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Bambo ake ndi `Abdullāh mwana wa `Abdul-Muttalib, ndipo mai ake ndi Āminah mwana wa Wahab. Mtundu wawo (awiriwa) umakumanizana pa agogo ake achisanu. Atate ake adamwalira Iye akadali mmimba mwa mai ake.

(3) KUBADWA KWAKE NDI KUYAMWITSIDWA KWAKE

1) Iye (s.a.w) anabadwira ku Makkah tsiku lolemba pa 12, mwezi wa Rabi`ul-Awwal, chaka cha njovu.

2) Ndipo chaka cha kubadwa kwake chidatchedwa kuti "**chaka cha njovu**", chifukwa chakuti mfumu ya Habashah idatumiza – mchaka cha kubadwa kwakechi – gulu la nkhondo ku Makkah kuti likagumule Ka`bah, ndipo mgululo mudali njovu yaikulu. Chomwecho Allah adaliwononga (gululo) pofuna kulemekeza kubadwa kwa Mtumiki (s.a.w).

3) Ndipo amene adamuyamwitsa Iye – pambuyo pa mai ake – ndi Thuwaybah wa mtundu wa Aslamiyyah, wantchito wa malume ake Abū Tālib. Ndipo kenako Hālimah wa mtundu wa Sa`diyyah, mpakana pamene nsinkhu wake udafika zaka zinai (4).

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) anabadwa liti? Nanga anabadwira kuti? Nchifukwa chiani chaka chomwe anabadwa chimatchedwa "chaka cha njovu?". Ndani yemwe adamuyamwitsa Iye pambuyo pa mai ake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

(Iye) anabadwira ku Makkah chaka cha njobvu. Ndipo adamuyamwitsa Iye Thuwaybah wa mtundu wa Aslamiyyah, ndipo kenako Hālimah wa mtundu wa Sa`diyyah.

(4) KUMWALIRA KWA MAI AKE NDI KUYANG'ANIRIDWA KWAKE

1) Adamwalira mai ake (s.a.w) Iye ali mchaka cha chisanu ndi chimodzi (6) cha kubadwa, pamene iwo amabwerera kuchokera ku Madinah.

2) Ndipo Iwo adapita ku Madinah kukayendera manda a atate ake ndipo adali limodzi ndi agogo ake a `Abdul-Muttalib[1].

3) Ndipo ndithu Iwo adayikidwa ku Abwā', mudzi omwe uli pakati pa Makkah ndi Madinah.

4) Chomwecho adamuyang'anira Iye Ummu Ayman, wantchito wa atate ake a `Abdullāh.

MAFUNSO

Kodi Mai ake adamwalira liti? Nchifukwa chiani Iwo adapita ku Madinah? Anayikidwa kuti? Ndi ndani yemwe adamulera pambuyo pa Mai ake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mai ake adamwalira iye ali ndi zaka zisanu ndi chimodzi (6) ndipo adayikidwa ku Abwā'. Chomwecho adamulera Iye ndi Ummu Ayman wantchito wa bambo ake.

[1] Ena amafotokoza kuti panthawiyi adali limodzi ndi Ummu Ayman (Amake Ayman), ndipo iye ndi amene anabwerera naye Mtumiki (s.a.w) ku Makkah.

(5) KULELEDWA KWAKE NDI KUMWALIRA KWA AGOGO AKE

1) Adagwira ntchito yomulera ndi kumukuza – pambuyo pa Mai ake – , agogo ake a `Abdul-Muttalib. Ndipo anali kumukonda zedi kuposa chikondi chawo pa ana awo.

2) Ndipo pamene zaka zake (s.a.w) zidakwana zisanu ndi zitatu (8), agogo ake adamwalira pambuyo pa kumuyang'anira kwa zaka ziwiri zokha.

3) Pambuyo pa kumwalira kwa agogo ake, adamuyang'anira Iye ndi malume ake Abū Tālib. Ndipo Iwo anali osawuka, chomwecho Allah adawachulukitsira phoso lawo.

4) Ndipo adali Iye (s.a.w) – mnyengo ya kuyang'aniridwa ndi malume ake – , okhutira ndi zomwe Allah wamugawira ndi kumufewetsera.

MAFUNSO

Ndani yemwe adamuyang'anira Iye (s.a.w) pambuyo pa kumwalira kwa Mai ake? Kodi Agogo ake adamwalira liti? Ndani adamuyang'anira pambuyo pa kumwalira kwa Agogo ake? Kodi kakhalidwe kake kadali kotani munthawi ya kuyang'aniridwa ndi malume?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adamulera Iye (s.a.w) – pambuyo pa mai ake – , agogo ake `Abdul-Muttalib, ndipo adamwalira agogo ake ali ndi zaka zisanu ndi zitatu (8), chomwecho adamuyang'anira ndi Abū Tālib.

(6) KUWETA KWAKE NKHOSA NDI ULENDO WAKE OYAMBA WA KU SHĀM (SYRIA)

1) Anali Iye (s.a.w) – mu umwana wake – kuweta mbuzi ndi nkhosa za anthu a pa Makkah, pa malipiro omwe amadzithandizira pa moyo wake.

2) Ndipo pamene adafika zaka zisanu ndi zinai (9)[2] adachita ulendo opita ku Shām (Syria) limodzi ndi malume ake Abū Tālib kukachita malonda.

3) Ndipo pamene adayandikira dera la Busrā, m'busa (otchedwa) Bahīrā adamuona Iye (s.a.w), chomwecho adafotokozera malume ake kuti Iye adzakhala otsiriza wa Aneneri (a.s). Ndipo adawapempha kuti abwerere naye powopera adani omwe angakhale tcheru kuyembekezera (kumuchita chiwembu).

4) Ndipo Iye (m'busa Bahīrā) adagwiritsira ntchito umboni pa utumiki wake (s.a.w) kudzera mzizindiro zake zomwe zili mmabuku a eni buku (Ayuda ndi Akhirisitu).

MAFUNSO

Kodi Iye (s.a.w) adali kugwira ntchito yanji mu umwana wake? Kodi ndi nthawi iti yomwe adapita ku Shām? Kodi adali ndi ndani pa ulendowu? Ndani yemwe adamuona Iye mu ulendo wake oyamba? Kodi adawauza chiani malume ake? Nanga adawapempha kuti atani? Kodi adagwiritsira umboni wanji pa za utimiki wake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Iye (s.a.w) mu ubwana wake anali kudyetsa mbuzi ndi nkhosa za anthu a pa Makkah, ndipo adakhala pa ulendo opita ku Shām limodzi ndi malume ake ali ndi zaka zisanu ndi zinai (9) kapena khumi ndi zitatu (13). Ndipo adamuona Iye (s.a.w) m'busa Bahīrā ndipo adazindikira pa Iye zizindikiro za uneneri.

[2] Ena amati adali ndi zaka khumi ndi zitatu (13) panthawiyi.

(7) ULENDO WAKE WACHIWIRI KUPITA KU SHĀM (SYRIA)

1) Mchaka cha chisanu ndi makumi awiri (25) mmoyo wake (s.a.w), Iye adapita ku Shām kachiwiri ndi malonda a mai olemekezeka Khadījah (r.a).

2) Ndipo Iye (Khadījah) anali mzimai wa ulemelero ndi chuma; amalemba ntchito amuna pa chuma chake.

3) Ndipo ndithu adamusankha Iye (s.a.w) pa ntchito imeneyi, chifukwa chakuti Iye adamva za chilungamo chake ndi kukhulupirira kwake komanso makhalidwe ake apamwamba.

4) Ndipo adali limodzi naye wantchito wake Maysarah, chomwecho adagula ndi kugulitsa ndipo awiriwo adabwerera ndi phindu lalikulu[3].

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe adapita ku ulendo wake wachiwiri ku Shām? Nchifukwa chiani adayenda ulendo umeneu? Kodi mai Khadījah adali mai otani? Nchifukwa chiani Iye (Khadījah) adamusankha Mtumiki (s.a.w) pa ntchito imenei? Ndani yemwe adayenda naye limodzi pa ulendo umeneu?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo Iye (s.a.w) adapita ku Shām kachiwiri zaka zake zili zisanu ndi makumi awiri (25), kukagulitsa malonda a mai Khadījah. Ndipo Iye (mai Khadījah) adali mai wachuma ndi ulemelero. Ndipo (mu ulendo umeneu) anali limodzi ndi wantchito wake Maysarah.

[3] Zikunenedwa kuti mu ulendo umenewu adamuona Iye (s.a.w) m'busa Nus̲tūrā, chomwecho adamuzindikira kuti Iye (s.a.w) ndi Mneneri yemwe akuyembekezeredwa.

(8) UKWATI WAKE NDI MAI KHADĪJAH (R.A)

1) Miyezi iwiri pambuyo pa kubwerera kwake ku ulendo wake wachiwiri, Iye (s.a.w) adakwatira mai Khadījah (r.a), ndipo Iye ndi amene adamufunsira banja (Mtumiki s.a.w).

2) Ndipo Iye (Khadījah) adali ndi zaka makumi anai (40) za kubadwa, pomwe Iye (s.a.w) anali ndi zaka zisanu ndi makumi awiri (25) za kubadwa.

3) Ndipo Iye (Khadījah) adali atakwatiwapo ndi Abī Hālah (bambo ake a Hālah), omwe adamwalira ali ndi mwana mwa Iye (Khadījah) dzina lake Hālah[4].

4) Ndipo Iye (Khadījah) adakhala pa banja ndi Mtumiki (s.a.w) zaka zisanu ndi makumi awiri (25), ndipo sadakwatire mkazi wina mpakana Iye (Khadījah) atamwalira.

MAFUNSO

Kodi Iye (s.a.w) adamkwatira Khadījah liti? Kodi adali ndi zaka zingati pamene amakwatiwa ndi Mtumiki (s.a.w)? Kodi nanga Iye (s.a.w) zaka zake zidali zingati? Kodi mai Khadījah adali atakwatiwapo ndi ndani asadakwatiwe ndi Mtumiki (s.a.w)? Kodi adakhala zaka zingati ndi Mtumiki (s.a.w)?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Miyezi iwiri chibwerereni ku ulendo wake adakwatirana ndi mai Khadījah – ndipo adali ndi zaka makumi anai – , pambuyo pa mamuna wake oyamba Abī Hālah. Ndipo adakhala ndi Iye (s.a.w) zaka zisanu ndi makumi awiri.

[4] Zimanenedwa kuti dzina lake lidali Hind.

(9) KUWERUZA KWAKE PAKATI PA MA QURAYSH ZA KUIKA MWALA WAKUDA

1) Mchaka cha chisanu ndi makumi atatu (35) cha kubadwa kwake, ma Quraysh adagumula Ka`bah ndikumanganso kachiwiri makoma ake.

2) Ndipo Iye (s.a.w) adatenga nawo gawo mu kumangaku, ndipo anali kunyamula nawo miyala limodzi ndi akulu-akulu a maquraysh, ndipo adali limodzi ndi malume ake Abbās (r.a).

3) Ndipo maquraysh adasiyana maganizo pa za munthu yemwe angayike mwala wakuda pa malo ake. Ndipo kenako adagwirizana kuti oweruza pakati pawo akhale aliyense oyambilira kulowa mumsikitimo.

4) Chomwecho oyambilira kulowa adali Mtumiki wa Allāh (s.a.w), ndipo chomwecho maquraysh adasangalala ndipo adati: "**Takondwera ndi okhulupirika**".

5) Chomwecho Iye (s.a.w) adaika mwalawo pa nsalu ndipo adapempha kwa mtsogeleri aliyense kuti agwire nsonga ya nsaluyo, ndipo kenako adawalamura kuti ayinyamule, ndipo pamene adafika nawo pa malo ake, Iye (s.a.w) adawutenga ndi dzanja lake nawuyika ndi dzanja lake lolemekezeka (pa malo pake). Pakutero kusagwirizana konse kudatheratu chifukwa cha kuweruza kwake, ndipo maquraysh anadodoma ndi kaganizidwe kake kamphamvu.

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe maquraysh adamanganso kachiwiri chipupa cha Ka`bah? Kodi Iye (s.a.w) adatenga nawo gawo? Kodi Iwo (maquraysh) adasemphana maganizo pa chiani? Kodi oyambilira kulowa adali ndani? Kodi adagamula bwanji pakati pawo?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adafika zaka zisanu ndi makumi atatu (35) adamanganso kachiwiri maquraysh nyumba ya Ka`bah, ndipo adamupanga Iye kukhala oweruza pa kuika mwala wakuda pa malo ake. Chomwecho adaweruza molungama ndi kugamula motsogoleledwa (ndi Allah).

(10) KUKULA KWAKE (S.A.W)

1) Adadziwika Iye (s.a.w) – pakati pa anthu ake – ndi mbiri zonse zotamandika, monga; kunena zoona, kukhulupirika, kufatsa, manyazi, kudzichepetsa, mpakana adamutcha kuti "**okhulupirika**".

2) Ndipo anthu ake ndi abale ake adali kumukonda chikondi choposa, ndipo adali kumulemekeza kulemekeza kopyola muyeso.

3) Ndipo Allah adamuteteza (Iye) kuyambira ku ubwana wake – ku zochita za umbuli. Chomwecho Iye sadamwepo mowa ndiponso sadalambirepo fano.

4) Ndipo Allah adamulemekeza Iye – asadalandire utumiki – ndi zozizwitsa zosiyana-siyana, zomwe zidasonyeza kukula kwa tsogolo lake, zina mwa izo ndi monga; kumutumizira kwake mtambo (omwe umamulondola ndi kumuphimba ku dzuwa) mu ulendo wake wachiwiri ku Shām.

MAFUNSO

Kodi adatchuka ndi chiani pakati pa anthu ake? Kodi anthu ake adali kumukonda? Kodi amachita nawo zomwe amachita anthu ake? Kodi Allah adamulemekeza ndi chiani asadalandire utumiki?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adadziwika mukukula kwake ndi mbiri za pamwamba. Ndipo anthu ake anali kumukonda, ndipo Allah adamuteteza Iye ku zochita za umbuli.

(11) MOYO WAKE PATANGOTSARA PANG'ONO KULANDIRA UTUMIKI

1) Pamene adayandikira zaka makumi anai (40) za moyo wake, adakonda kutalikirana ndi anthu ndi kuchita mapemphero (kupembedza).

2) Ndipo adakusankhira kupembedza kwakeko phanga la Hirā', lomwe ndi phiri mnjira yopita ku Makkah.

3) Ndipo anali kutenga limodzi ndi Iye phoso lake, ndipo likatha amabwerera kwa mkazi wake Khadījah kukatenga lina.

4) Ndipo adali kupembedza mogwirizana ndi chipembedzo cha agogo ake Ibrāhīm (a.s); kuyambira masiku khumi mpakana mwezi.

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe adayamba kukonda kutalikirana ndi anthu? Kodi adali kupembedza kuti? Kodi amadya kuchokera ku chiani? Kodi adali kupembedza pa chipembedzo chiti? Kodi kupembedza kwake kumatenga nthawi yochuluka bwanji?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adayandikira zaka makumi anai (40), adakonda kukhala yekha-yekha. Ndipo adali kupembedza ku phanga la Hirā' mogwirizana ndi chipembedzo cha Ibrāhīm (a.s).

KUFOTOKOZA MWACHIDULE GAWO LOYAMBA (LOYENERA KULOWEZA)

Bwana wathu Muhammad (s.a.w), mwana wa `Abdullāh ndi Āminah wa chiquraysh. Iye ndi omaliza wa Aneneri komanso Mtumiki wa Allāh kwa anthu onse, kuti amupembedze Iye yekha basi ndipo asamuphatikize ndi chilichonse.

Ndipo ndithu Iye anabadwira pa Makkah, lolemba pa 12 mwezi wa Rabī`ul Awwal. Ndipo bambo ake adali atamwalira kale Iye asanabadwe ndipo adayikidwa ku Madinah. Chomwecho adamulera mai ake, ndipo adamuyamwitsa Thuwaybah wa mtundu wa Aslamiyyah, ndipo kenako Halīmah wa mtundu wa Sa`diyyah.

Ndipo mchaka cha chisanu ndi chimodzi (6) cha kubadwa kwake, mai ake adamwalira ku Abwā', chomwecho adamusamalira Iye Ummu Ayman, ndipo adamuyang'anira Iye agogo ake. Ndipo mchaka cha chisanu ndi chitatu (8) cha kubadwa, adamwalira agogo ake chomwecho adamuyang'anira malume ake Abū Tālib.

Ndipo mchaka cha chisanu ndi chinai (9) adayenda ulendo ndi malume ake Abī Tālib kupita ku Shām, ndipo adamuona Iye (s.a.w) m'busa Bahīrā choncho adamuzindikira.

Ndipo mchaka cha chisanu ndi makumi awiri (25) adayenda ulendo pa malonda a mai olemekezeka Khadījah (r.a), ndipo miyezi iwiri pambuyo pa kubwererako adakwatirana naye, ndipo zaka zake zidali makumi anai (40).

Ndipo mchaka cha chisanu ndi makumi atatu (35) mmoyo wake adatenga nawo gawo pa kumanga Ka`bah, ndipo adaweruza pakati pawo za kuika mwala wakuda pamalo pake.

Ndipo adatchuka pakati pa anthu ake ndi mbiri zabwino, ndipo adali kumukonda ndi kumulemekeza kotero kuti adamutcha "**okhulupirika**".

Ndipo Allāh adamuteteza ku zochita za umbuli, ndipo adakonda kutalikirana ndi anthu pamene adayandikira zaka makumi anai (40) za moyo wake. Ndipo Iye adali kupembedza ku phanga la Hirā' mogwirizana ndi chipembedzo cha Ibrāhīm (a.s).

GAWO LACHIWIRI: KUCHOKERA MMOYO WAKE (S.A.W)

(12) CHIYAMBI CHA KUTSIKA KWA CHIVUMBULUTSO (WAHY)

1. Pamene Iye adafika zaka makumi anai (40) mmoyo wake, Allah adamutumiza Iye kukhala opereka nkhani yabwino ndi mchenjezi, ndi oyitanira ku choonadi mwachilolezo chake, ndi nyali yowunika.

2. Ndipo (chivumbulutso) chidayambidwa kwa Iye ndi maloto owona, chomwecho samaona chinthu kutulo kwake koma chimachitikadi (masomphenya) akadzuka.

3. Ndipo kenako udatsika kwa Iye mzimu okhulupirika (Jibrīl a.s), Iye (s.a.w) akupembedza ku phanga la Hirā'.

4. Ndipo adamphunzitsa Iye momwe angawawongolere anthu ku njira yowongoka, ndi kuwatsogolera ku kutsatira chipembedzo cholungama.

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe adatumizidwa Iye (s.a.w)? Kodi chivumbulutso chidayambika bwanji? Kodi ndi ndani yemwe adatsika kwa Iye ndi chivumbulutso? Kodi ndi kuti komwe chivumbulutso chidamtsikira? Kodi Jibrīl adamutsikira Iye kuti? Nanga adamphunzitsa chiani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Allah adamutumiza Iye kwa anthu pa nsonga pa zaka makumi anai (40), ndipo chivumbulutso chidayambika kwa Iye ndi maloto abwino (owona).

(13) KAKHALIDWE KA ALUYA CHISADAFIKE CHISILAMU

1. Anali aluya asadalandire chisilamu ophatikiza Allah ndi zinthu zina, amapembedza mafano ndi kuwayeretsa (kuwalemekeza).

2. Ndipo anali kupha ana awo chifukwa cha kuopa njara ndi umphawi.

3. Ndipo anali kukwirira mdothi ana awo akazi amoyo, chifukwa cha kuopa kuyaluka ndi kunyozeka.

4. Ndipo adali osagwirizana ndi okangana (nthawi zonse); kumamenyana nkhondo pakati pawo pa zifukwa zopanda pake.

MAFUNSO

Kodi aluya amapembedza chiani chisilamu chisadafike? Kodi nchifukwa chiani adali kupha ana awo? Nchifukwa chiani adali kukwirira mdothi ana awo akazi? Kodi anali ogwirizana?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adali aluya asadatumizidwe Iye (s.a.w) odana, osagwirizana; ena a Iwo kumamenya makosi a ena (kuphana). Ndipo ambiri a Iwo adali opembedza mafano. Amapha ana awo achimuna ndi achikazi.

(14) KUYITANIRA MOBISA

1. Adayamba Mneneri (s.a.w) kuyitanira mobisa pamene adatsika (kwa Iye) mau akuti: **Eh! Iwe amene wadziphimba nsalu! Imirira ndipo uwachenjeze anthu (ako). Ndipo Mbuye wako yekha umkulitse. Ndipo nsalu zako uziyeretse. Ndiponso zoipa zipewe. Usapatse (anthu) ncholinga choti ulandire zambiri. Ndipo chifukwa cha Mbuye wako, pirira**".

2. Chomwecho Iye adawaitanira abale ake ndi omwe adali kuwakhulupirira mwa anzake amene adali kukhulupirira za kuwona kwake.

3. Adawaitanira ku kumpembedza Allah yekha basi, ndi kuchitira chisoni anthu, ndi umodzi komanso kusiya nkhondo.

4. Ndipo Iye adayamba kuitanira mwachinsinsi powopa kuwadzidzimutsa anthu ndi chinthu chomwe sadachidziwepo ndi kuchimvapo (kale lonse).

MAFUNSO

Kodi kuitanira mobisa kudayamba liti? Ndi ndani omwe adawaitanira mobisa? Kodi amawaitanira ku chiani? Nanga nchifukwa chiani adayamba kuitanirako mobisa?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Iye adayamba kuitanira mobisa, chomwecho adawaitanira abale ake ndi banja lake ku umodzi (wa Allah), ndi kugwirizana ndi kukhala ofewa kwa ofowoka.

(15) OYAMBA WA OKHULUPIRIRA

1. Oyamba yemwe adamukhulupirira Iye mwa akazi, ndi Khadījah. Ndipo Iye adali kukhulupirira kuona kwa utumiki wake chifukwa cha zomwe zidaonekera kwa Iye mzizindikiro zosonyeza uneneri wake kuchokera pa ulendo wake ndi watchito wake Maysarah.

2. Ndipo oyambirira yemwe adamukhulupirira Iye mwa amuna ndi Abūbakr Siddīq (r.a)[5], ndipo adali bwenzi lake asatumizidwe (ngati Mtumiki). Ndipo sadawonepo pa Iye bodza lililonse, ndi Zaid mwana wa Hārithah (r.a), ndipo Iye adali kapolo wa Mtumiki (s.a.w) chomwecho adammasula (kumpatsa ufulu).

3. Ndipo oyambilira yemwe adamkhulupirira Iye mwa ana ndi `Alī (r.a) mwana wa Abī Tālib. Ndipo Iye adali mwana oleledwa ndi Mtumiki (s.a.w).

4. Ndipo Abūbakr (r.a) adayitanira omwe anali kuwakonda ndi kumukonda Iye, chomwecho lidavomera gulu lambiri la Iwo omwe ena a Iwo ndi; `Uthmān mwana wa `Affān (r.a)[6] wachitatu wa otsogoleri olungama, ndi Zubayr mwana wa `Awwām (r.a).

MAFUNSO

Kodi ndani oyamba kumukhulupirira Iye mwa akazi? Kodi ndani oyamba kumukhulupirira Iye mwa amuna? Kodi ndani oyamba kumukhulupirira Iye mwa ana? Nchiani chomwe Abu Bakr adachita pambuyo pa kulandira kwake chisilamu?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Oyambirira kumkhulupirira Iye ndi olemekezeka Mai Khadijah, ndi Abu Bakr Siddiq, ndi Ali. Ndipo kenako Abu Bakr adaitanira anzake monga Uthman mwana wa Affan ndi Zubayr mwana wa Awwam ndipo chomwecho adakhulupirira.

[5] Ndipo Iye adali odzisunga ndi opereka zedi, pachifukwa chimenechi adali ngati nduna kwa Mtumiki (s.a.w) yomwe amaifunsa maganizo pa zinthu (zosiyana-siyana).

[6] Ndipo pamene amalume ake (al-Hakam) adadziwa za kulandira kwake chisilamu adamumangirira ndi zingwe, ndipo adati; "Zoona ukusiya chipembedzo cha makolo ako ndi kutsatira chipembedzo chopekedwa?. Ndikulumbira Mulungu, sindikumasula mpakana usiye zomwe Iwe uli pa izo. Chomwecho Uthmān adati kwa Iwo: "Ndikulumbira Allah, sindichisiya (chipembedzo chimenechi) kapena kulekana nacho". Chomwecho pamene Iwo adaona kulimba kwake adamusiya. Zikufokotozedwanso kuti; "Iwo adali kumufukitsira utsi uku atamangidwa ndi zingwe kuti abwerere ku chipembedzo cha mafano, koma Allah adampatsa mphamvu zolimbangana (pa chisilamu)".

(16) KUYITANIRA MOWONETSERA

1. Kudapitirira kuitanira mobisa zaka zitatu, ndipo adavomera mkati mwakuitanira kumeneku ambiri mwa anthu olemekezeka komanso akapolo.

2. Pambuyo pa zimenezi adalamuridwa Iye (s.a.w) za kuwonetsera poyera kupyolera mmau a Allah wapamwamba-mwamba onena kuti: "**Chomwecho lengeza zimene ukulamulidwa, ndipo uwapewe anthu opembedza mafano**".

3. Chomwecho adakwera pa phiri la Safā ndipo adawaitana anthu ake. Ndipo pamene adasonkhana adati kwa Iwo: "**Kodi mundikhulupirira pa zomwe ndikuwuzeni?**". Ndipo onse adati: "**Inde, sitidayambe tamvapo bodza kwa Iwe chiyambireni kukula kwako mpaka lero**". Chomwecho Iye (s.a.w) adati: "**Dziteteni nokha ku moto, ndithu Ine ndi mchenjezi wanu ku chilango chachikulu**".

4. Chomwecho malume ake adati kwa Iye: "**Kuwonengeka kukhale pa Iwe Muhammad! Zowona watisonkhanitsa chifukwa cha zimenezi?!**" Choncho Allah adavumbulutsa Sūrah Lahab pa nkhani ya Iwo: "**Awonongeka manja a Abī Lahab, ndipo nayenso wawonongeka**"……, mpakana kumapeto….

MAFUNSO

Kodi kudapitirira zaka zingati kuitanira mobisa? Kodi ndi nthawi iti yomwe adawonetsera poyera kuitanira? Kodi adawonetsera motani? Kodi malume ake adati chiani kwa Iye?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pambuyo pa zaka zitatu adalamulidwa za kuwonetsera poyera, chomwecho adawasonkhanitsa anthu ake ndipo adawachenjecza za chilango cha moyo omaliza.

(17) KUSONKHANITSA KWAKE ABALE AKE

1. Adasonkhanitsa Mneneri (s.a.w) banja lanje ndi abale ake pamene adavumbuluka kwa Iye mau ake (Allah) wapamwamba-mwamba (akuti): "**Ndipo achenjeze abale ako apafupi**".

2. Chomwecho adawafikitsira uthenga wa Mbuye wake[7], ndipo adawachenjeza za chilango cha tsiku lalikulu: "**tsiku lomwe chuma ndi ana sizidzathandiza (aliyense)**".

3. Chomwecho anthuwo adayankha mau ofewa, kupatula Abū Lahab yemwe adali mdani wake oyipitsitsa.

4. Pakuti ndithu Iye adayankha yankho loipa ndipo adawalamura anthuwo kuti amugwire (ndikumumanga). Koma Abū Tālib adati kwa Iye: "Ndikulumbira Mulungu, ndithudi timuteteza pamene tili moyobe".

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe Mneneri adawasonkhanitsa abale ake? Kodi adati chiani kwa Iwo? Nanga adamuyankha zotani? Kodi Abu Lahab adamuyankha chiani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adatsika mau ake (Allah) wapamwamba-mwamba (onena kuti): "**Ndipo chenjeza abale ako apafupi**", Iye (s.a.w) adasonkhanitsa banja lake ndi abale ake, ndipo adawafikitsira uthenga wa Mbuye wake. Chomwecho malume ake Abū Lahab adamuyankha Iye yankho loipa zedi.

[7] Iye adati kwa Iwo: "Ndithu nthumwi ya anthu siinamiza anthu ake, ndipo ndikulumbira Allah ngati nditawanamiza anthu onse koma inuyo sindingakunamizeni. Ndipo ngati nditawachita chinyengo anthu onse koma inuyo sindingakuchiteni chinyengo. Ndikulumbira Allah yemwe palibe mulungu wina koma Iye basi, ndithu Ine ndi Mtumiki wa Allah kwa inu mwapadera-dera ndi anthu onse pamodzi. Ndikulumbira Allah, ndithudi mudzamwalira monga momwe mumagonera ndipo ndithudi mudzadzutsidwa (tsiku la chiweruzo) monga momwe mumadzukira kutulo. Ndipo mudzawerengedwa pa zomwe mumachita, ndipo mudzalipidwa zabwino pa kuchita kwanu zabwino, ndiponso zoipa pa kuchita kwanu zoipa. Ndipo ndithudi iwo ndi munda wamtendere mpaka muyaya, kapena moto mpaka muyaya".

(18) KUSONKHANA KWA MAQURAYSH POLIMBANA NDI MTUMIKI (S.A.W)

1. Chidasintha chikondi cha ma Quraysh kwa Mtumiki (s.a.w) kukhala udani, ndi kufupikirana naye kwawo kukhala kutalikirana, ndi kuyankhula kwake zoona kukhala bodza, ndi zochita zake kukhala chibwana.

2. Zimenezi (zidachitika) kuyambira pamene Iye adawaitanira ku kupembedza Allah, ndi kutchula zofowoka za milungu yawo, ndi pamenenso adamutcha aliyense oyipembedza (milunguyo) kuti ndi osochera.

3. Ndipo ndithu Iwo adapita kwa malume ake (Abī Tālib) ndikuwapempha kuti amuletse Mtumiki (s.a.w) kusambula milungu yawo ndi kuwanena makolo awo kuti ndi osochera[8].

4. Chomwecho Iwo (Abū Tālib) adawayankha yankho labwino, uku Mtumiki (s.a.w) akupitirirabe kufalitsa chipembedzo ndi kukweza liwu la chowonadi.

MAFUNSO

Kodi chikondi cha maquraysh kwa Mtumiki chidawonjezekera pambuyo pa kupatsidwa kwake utumiki? Kuchokera nthawi yanji? Kodi iwo adawapempha malume ake kuti amuletse? Kodi adawayankha zotani?

[8] Iye sadawatche Iwo kuti ndi osochera kapena kuwasimba kuti ndi opanda nzeru ndi chiwongoko, koma pambuyo pakuti adakakamirabe umboni wakuti akutsatira za makolo awo. Allah wapamwamba-mwamba akuyankhula kuti: “Ndipo kukanenedwa kwa Iwo kuti; “Tsatirani zomwe Allah wabvumbulutsa”, Iwo amati: “Koma tikutsa zomwe tidawapeza nazo atate anthu”. Kodi ngakhale kuti atate awo sadali ozindikira chilichonse ndiponso sadali owongoka (awatsatirabe)?

(19) KUBWERA KWA MAQURAYSH KWA ABĪ TĀLIB KACHIWIRI

1. Pamene maquraysh adaona kupitirira kwa Mtumiki (s.a.w) pa kufalitsa kuyitanira kwake ndi kumuyimira kwa malume ake, adayenda kupita kwa malume ake kachiwiri.

2. Ndipo adati kwa Iwo: "Ndithu Ife sitikupirira ndi kusambulidwa kwa makolo athu, ndi kunyoza nzeru zathu, ndi kutoza milungu yathu. Chomwecho uyenera kumuletsa mwana wa m'bale wako kapena utilole kumuletsa (tokha)".

3. Chomwecho malume ake adamuitana Iye (s.a.w) ndikumupempha kuti asiye, pomuwopera maquraysh, chomwecho Iye adakana.

4. Ndipo adati[9]: "**Ndikulumbira Allah, sindingasiye chinthu ichi kufikira Allah achipambanitse kapena Ine ndiwonongeke pambali pake**".

5. Chomwecho malume ake adati kwa Iye: "Pita ndipo kanene zomwe ungakonde, pakuti ndikulumbira Allah, sindidzakupereka (kwa adani ako) mpaka kale-kale".

MAFUNSO

Nchifukwa chiani maquraysh adapita kwa Abī Tālib kachiwiri? Adati chiani kwa Iwo? Kodi malume ake adamuletsa? Kodi Mtumiki (s.a.w) adayankha zotani? Nanga malume ake adamuyankha zotani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adayenda maquraysh kupita kwa malume ake kachiwiri kuti akamuletse kusambula milungu yawo koma sadakwanitse kumuletsa. Ndipo Iye adapitirira mnjira yake (yoitanira).

[9] Adati: "Ndikulumbira Allah, E! Inu malume anga! Ngakhale akadaika dzuwa kudzanja langa la manja, ndi mwezi kudzanja langa la mazere kuti ndisiye chinthu ichi, sindikadachita zimenezo kufikira Allah achipambanitse kapena ndiwonongeke pambali pake".

(20) KUBWERA KWA MAQURAYSH KWA ABĪ TĀLIB KACHITATU

1. Pamene ma Quraysh adaona kuti Abā Tālib sakufuna kumuletsa mwana wa m'bale wawo, adayenda kupita kwa Iwo limodzi ndi `Umārah mwana wa al-Walīd.

2. Ndipo adati: "Tenga mnyamata uyu kukhala mwana wako, ndipo umpereke kwa Ife mwana wa m'bale wako kuti timuphe.

3. Chomwecho malume ake adati: "Chiyipirenji chomwe mukufuna (kwa Ine). Zowona mukundipatsa mwana wanu kuti ndimulere, pomwe Ine ndikupatseni mwana wanga kuti mumuphe?".

4. Chomwecho adabwerera manja-manja, uku Mtumiki (s.a.w) akupitirizabe kufalitsa chisilamu ndipo malume ake akumuyimirabe.

MAFUNSO

Nchifukwa chiani maquraysh adapita kwa Abī Tālib kachitatu? Adati chiani kwa Iwo? Kodi Iwo adawayankha zotani? Kodi Mtumiki (s.a.w) adasiya kuitanira?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adayenda maquraysh kupita kwa malume ake kachitatu, ndipo adawapempha kuti amupereke kwa Iwo kuti amuphe. Chomwecho Iwo adawapeputsa nzeru zawo.

(21) KUPEREKA MASAUTSO KWA MAQURAYSH PA MTUMIKI (S.A.W)

1. Maquraysh adayamba kumusawutsa Mtumiki (s.a.w) ndi kumuchita chipongwe makamaka pamene akupita kukapemphera. Pambuyo pakuti adaona kupitiriza kwake kuitanira ndi kumuyimira kwa malume ake.

2. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adali kuwabwezera ndi kudekha, ndi kupirira, ndi kuleza, ndi kukhululuka.

3. Ndipo yemwe adali oipitsitsa zedi pa kumuvutitsa Mtumiki (s.a.w) adali Abū Jahl[10] ndi Abū Lahab[11] ndi `Uqbah mwana Abī Mu`ayṭ ndi al-Walīd[12] mwana wa al-Mughīrah.

4. Ndipo ndithu Allah adawalanga[13] onse omuchita Iye (s.a.w) chipongwe pambuyo pa nsamuko, chomwecho ena a Iwo anaphedwa, ndipo ena a Iwo adawononged wa ndi nthenda zosiyana-siyana.

MAFUNSO

Nchiani chomwe adachita maquraysh pamene adaona kupitirira kwa Mtumiki pa kufalitsa kuyitanira? Ndi kumuyimira kwa malume ake? Kodi Mtumiki adali kuwabwezera ndi chiani? Ndani yemwe adali oipitsitsa pa kumuvutitsa Mtumiki (s.a.w)? Kodi Allah adawalanga ochita chipongwe?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Maquraysh adayamba kumusawutsa Mtumiki (s.a.w), ndipo Iye adali kuwabwezera ndi kuleza ndi kupirira. Ndipo adani ake oipitsitsa anali Abū Jahl, Abū Lahab ndi `Uqbah mwana wa Abī Mu`ayṭ.

---

[10] Zina mwa izo nzakuti tsiku lina adamuona Mtumiki (s.a.w) akupemphera ndipo chomwecho adamuletsa, pamenepo Mtumiki (s.a.w) adamuyankhula mwa ukali ndikumuopseza. Abu Jahl adati: "Zoona ukundiopseza chikhalirecho ndine ochuluka zedi athandizi pa chigwa chino (cha Makkah)?" Pamepo Allah adavumbulutsa (mawu) omuchenjeza kuti: "Ayi ndithu, ngati sasiya timukoka tsitsi la pa tsumba. Tsumba labodza ndiponso lamachimo. Basi, aliyitane gulu lakelo, nafe tiyitana Azabaniya (angelo akumoto). Ayi ndithu, usamumvere koma gwetsa nkhope yako pansi ndipo udziyandikitse kwa Mbuye wako".

[11] Adali kuika nyasi pa khomo la Mtumiki (s.a.w), ndipo mwachitsanzo; adamuona Mtumiki (s.a.w) akupemphera ulendo wina chomwecho adamufinya pakhosi mwamphamvu. Ndipo Abubakr (r.a) adatulukira ndikumuleletsa kwa Iye ndipo adati; "Zoona mukumupha munthu chifukwa cha kunena kuti Mbuye wanga ndi Allah, chikhalirecho wakudzerani ndi maumboni ochokera kwa Mbuye wanu?"

[12] Iye ndi amene Allah akuyankhula za Iye kuti: "Ndisiye ndi amene ndidamulenga ndekha. Ndipo ndampatsa chuma chambiri. Ndi ana okhala nawo (paliponse)"….Ayah yodziwika..

[13] Ngati momwe akuyankhulira Iye wapamwamba-mwamba kuti: "Ndithu, Ife tikukwanira (kukuteteza) ku zoipa za achipongwe".

(22) KUPEREKA MASAWUTSA KWA MAQURAYSH PA MA SAHĀBAH (R.A)

1. Pamene maquraysh adaona kuti Mtumiki (s.a.w) wasanduka kukhala wamphamvu ndi olemekezeka, adasiya kumusawutsa.

2. Ndipo tsopano adatembenukira kwa ophunzira ake pakupereka masawutso, maka-maka ofowoka (mwa Iwo) omwe analibe owathandiza aliyense.

3. Chomwecho mtundu uliwonse udayamba kuwalanga omwe adalandira chisilamu mwa Iwo kudzera mkuwatsekera, kumenya, kuwakhazika ndi njala ndi ludzu, kotero kuti mmodzi wa Iwo adafika posakwanitsa kukhala pansi komanso osadziwa kuti anene chiani, chifukwa cha kukula kwa chilango.

4. Ndipo ena mwa omwe adalingidwa ndi Bilāl (r.a)[14], Ammār (r.a) mwana wa Yāsir (r.a)[15] ndi m'bale wake ndi bambo ake and mai ake, komanso Khabbāb (r.a) mwana wa Aratt[16].

MAFUNSO

Kodi maquraysh adasiya liti kumusawutsa Mtumiki (s.a.w)? Nanga adatembenukira kwa ndani ndi chilango chawo? Kodi adali kuwalanga motani? Tchulani odziwika kwambiri mwa omwe adalingidwa ndi kuzunzidwa?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene Mtumiki (s.a.w) adakhala ndi mphamvu maquraysh adayamba kulanga ophunzira ake, maka-maka ofowoka a Iwo monga; Bilāl ndi Ammār mwana wa Yāsir.

[14] Bwana ake a Umayyah adali kumumangilira chingwe mkhosi ndi kuchipereka kwa ana kuti adzisewera naye (kumamukoka) uku Iye akuyankhula kuti: "(Allah) ndi mmodzi, (Allah) ndi mmodzi". Ndipo amatuluka naye kupita ku mchenga otentha mwadzaoneni umene ngati dutswa la mnofu litaikidwa pa iwo lingathe kupsya, ndipo kenako amalamuro kuti chimwala chiikidwe pa mtima pake ndipo akatero amati kwa Iye: "Ukhala chomwechi mpakana umwalire kapena umukane Muhammad". Ndipo Iye adapitirirabe kuzunzika chomwechi kufikira pamene Abubakr adamugula ndi kumpulumutsa.

[15] Adali kumulanga ndi moto mpakana bambo ake a Ammār ndi mai ake adamwalira mkati-kati mwa chilango chimenechi.

[16] Bwana ake aakazi amabwera ndi chitsulo chotenthedwa pamoto ndikuchiika pansana pake kuti asiye chisilamu, koma zonsezi zimangomuonjezera chikhulupiriro.

(23) ZOFUNA ZA MAQURAYSH KWA MTUMIKI (S.A.W)

1. Pamene maquraysh adaona kuti kupereka mazunzo sikukupereka phindu lililonse, koma kuti kudawawonjezera Asilamu chikhulupiriro ndi chitsimikizo, adayenda[17] kupita kwa Mtumiki (s.a.w).

2. Ndipo adapempha kwa Iye kuti adzipembedza milungu yawo ndipo nawonso adzipembedza Mulungu wake. Chomwecho Allah adavumbulutsa kwa Iye Sūrah Kāfirūn.

3. Chomwecho pamene adataya mtima adamupempha Iye kuti achotse mu Qur'ān ndime zomwe zimawakwiyitsa zonyoza milungu yawo ndi kupembedza kwawo, kapena apo ayisinthe ndi Qur'ān ina.

4. Chomwecho Allah adavumbulutsa (mawu awa) powayankha: "**Nena, nkosatheka kwa Ine kuisintha mwachifuniro changa. Sinditsata china koma zomwe zikuvumbulutsidwa kwa Ine basi**".

MAFUNSO

Nchifukwa chiani maquraysh adapita kwa Mtumiki (s.a.w)? Nchiani chomwe adapempha kwa Iye? Allah adavumbulutsa chiani pofuna kuwayankha? Nchiani chomwe adapempha kwa Iye pambuyo pa zimenezo? Kodi Iye adawayankha kuti chiani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adataya mtima za Iye adamupempha kuti adzipembedza milungu yawo, nawonso adzipembedza Mulungu wake, kapena ayisinthe Qur'ān yomwe muli kusambula milungu yawo.

[17] Asadapite kwa Iye adamutumiza `Uqbah mwana wa Walīd, chomwecho adapita kwa Iye ndipo adati: "Eh! Mwana wa m'bale wanga! Ndithu Iweyo kwa Ife uli monga momwe ukudziwira – mmodzi wa abwino athu mu ulemelero ndi mtundu wa makolo. Ndipo ndithu Iwe wadza kwa anthu ako ndi chinthu chachikulu zedi chomwe wasiyanitsa nacho umodzi wawo, ndi kupeputsa nzeru zawo, ndikutoza milungu yawo ndi chipembedzo chawo, ndikuwatcha kuti osakhulupirira omwe adapita mwa makolo awo, chomwecho imva kwa Ine. Ngati ukufuna chuma tikusonkhanitsira mchuma chathu mpakana ukhala ochuluka zedi chuma pakati pathu. Ndipo ngati ukufuna ulemelero tikupatsa utsogoleri pa Ife. Ndipo ngati izi zomwe zikukufikira kuchokera muziwanda sitingathe kuzichotsa, tikuitanira dotolo kuti akuchize". Chomwecho pamene Iye adamaliza, Mtumiki (s.a.w) adamuwerengera kumayambiliro kwa Surah Fussilat, chomwecho `Uqbah adamutseka pakamwa pake ndipo adamupempha pempha kuti asiye kuwerengako. Ndipo pamene adabwerera adawalangiza anthu ake kuti amusiye, koma Iwo adakana kutero.

(24) NSAMUKO OYAMBA WA KU HABASHAH

1. Pamene Mtumiki (s.a.w) adaona zomwe zimawapeza ma Sahabah ake kuchokera mmazunzo ndi zilango zosiyana-siyana, adawalamura za kusamukira ku Habashah.

2. Chomwecho adasamuka khumi mwa ma Sahabah ake ndi azimai asanu, ena mwa Iwo ndi; `Uthmān (r.a) mwana wa `Affān ndi mkazi wake Ruqayyah (r.a) mwana wa Mtumiki (s.a.w).

3. Ndipo Iwo adabwererako pambuyo pa miyezi itatu chifukwa cha kuwawa kwa kukhala ku chilendo ndi kuchepa kwa chiwerengero chawo.

4. Ndipo zimenezi zidachitika mchaka cha chisanu chilandilireni utumiki, ndipo umenewu ndi nsamuko oyambilira mchisilamu.

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe Mtumiki (s.a.w) adalamura ma Sahabah ake za kusamukira ku Habashah? Kodi chiwerengero cha osamuka chinali chingati? Kodi adabwererako nthawi yanji? Kodi zimenezi zidachitika mchaka chanji?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene masawutso adakula pa asilamu, Mtumiki (s.a.w) adawalamula za kusamukira ku Habashah. Chomwecho adasamuka amuna khumi ndi akazi asanu, ndipo adabwerera pambuyo pa miyezi itatu.

(25) KULANDIRA CHISILAMU KWA HAMZAH NDI `UMAR (R.A)

1. Mchaka cha chisanu adalandira chisilamu anthu awiri mwa akulu-akulu a maquraysh, odziwika ndi mphamvu ndi nyonga.

2. Ndipo Iwo ndi Hamzah (r.a)[18]; malume ake a Mtumiki (s.a.w), ndi `Umar (r.a)[19] mwana wa Khattāb; wachiwiri wa atsogoleri olungama.

3. Ndipo `Umar (r.a) asadalandire chisilamu adali mmodzi wa akulu-akulu ochitsutsa chisilamu, ndi owalanga zedi omwe adalandira chisilamu, chomwecho Allah adachipatsa mphamvu chisilamu kupyolera mwa awiriwa.

4. Ndipo asilamu panthawiyi adali makumi anai (40) ndi akazi khumi ndi mmodzi (11).

MAFUNSO

Ndani omwe adalandira chisilamu mchaka cha chisanu? Ndani Iwo? Kodi `Umar adali otani asadalandire chisilamu? Kodi chiwerengero cha asilamu panthawiyi chinali chotani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka chachisanu cha utumiki Allah adachipatsa mphamvu chisilamu kupyolera mwa `Umar mwana wa Khattāb ndi Hamzah mwana wa `Abdul-Muttalib, malume ake a Mtumiki (s.a.w).

[18] Chifukwa cha kulowa kwake chisilamu nchakuti mdzakazi wina adamufotokozera Iye za kupereka mazunzo kwa Abu Jahl pa mwana wa m'bale wake (Muhammad s.a.w), chomwecho Iye adalunjika kupita komwe kudali munthu watsokayo (Abu Jahl) ndipo adakangana naye ndi kumunyoza. Ndipo adati: "Muhammad atukwanidwa bwanji kumachita kuti Ine ndili pa chipembedzo chake?". Chomwecho adalandira chisilamu ndipo chisilamu chake chinali chabwino zedi kotero kuti mpakana adatchedwa kuti "Mkango wa Allah".

[19] Palibe yemwe ankayembekezera kuti angalandire chisilamu, koma kuti Mtumiki (s.a.w) adayankhula mau – *patangotsala pang'ono kuti alandire chisilamu* - , onena kuti: "Eh! Allah! Chipatseni mphamvu chisilamu kudzera mwa Umar". Chomwecho madalitso a pempho la Mtumiki (s.a.w) adafika pa Iye.

(26) KUSALIDWA KWA MTUMIKI (S.A.W) NDI BANJA LAKE

1. Pamene maquraysh adaona kufalikira kwa Chisilamu mmafuko osiyana-siyana, adatsimikiza za kumupha Mtumiki (s.a.w).

2. Chomwecho adamusala (ndi kumupanikiza) ndi abale ake kumbali kwa mapiri ndipo adaletsa chakudya (chilichonse kuwafikira) Iwo, ndipo adagwirizana kuti asavomere pempho la chiyanjano lililonse kupatula ngati angamupereke Mtumiki (s.a.w) kuti aphedwe.

3. Ndipo adalemba zomwe adagwirizanazo pa chikalata chomwe adachipachika pa Ka`bah.

4. Ndipo zimenezi zidachitika mchaka cha chisanu ndi ziwiri (7) cha utumiki.

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe maquraysh adatsimikiza za kumupha Mtumiki (s.a.w)? Nanga adachita chiani za Iyeyo? Kodi adagwirizana pa fundo yanji? Kodi adalemba pangano lililonse? Kodi pangano limeneli lidali pamalo anji?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene chisilamu chidafalikira, maquraysh adamusala (ndi kumupanikiza) Mtumiki (s.a.w) ndi abale ake ndi ophunzira ake kumbali kwa mapiri a pa Makkah, ndipo adaletsa chakudya chilichonse kuwafika Iwo kwa zaka zitatu. Ndipo adagwirizana za kumupha Iye.

(27) NSAMUKO WACHIWIRI WA KU HABASHAH

1. Pambuyo pa kulowa kwa Mtumiki (s.a.w) ndi anthu ake kumbali kwa phiri kuja, Iye adalamura asilamu onse za kusamukira ku Habashah.

2. Chomwecho adasamuka amuna 73 ndi akazi 11, ena mwa Iwo ndi; Ja`far (r.a) mwana wa Abī Tālib.

3. Ndipo adakhala nawo Iwo limodzi asilamu a kuyemeni, omwe ndi Abū Mūsā al-Ash`arī (r.a) ndi ana a malume ake.

4. Ndipo nsamuko umenewu udachitika mchaka cha chachisanu ndi chiwiri (7) pambuyo pa utumiki.

MAFUNSO

Kodi Iye adalamura chiani ma Sahabah ake pambuyo pa kulowa kumbali ya mapiri? Kodi osamuka adali angati? Ndani omwe adakhala nawo limodzi Iwo? Kodi ndi chaka chanji chomwe udachitika nsamuko umenewu?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pambuyo pa kulowa kwa Mtumiki (s.a.w) ku mbali kwa phiri mchaka cha 7, adalamula Asilamu za kusamukira ku Habashah kachiwiri. Chomwecho adasamuka amuna 73 ndi akazi 11, ndipo adakhala nawo limodzi Iwo asilamu a kuyemeni.

(28) KULANDIRA CHISALAMU KWA MFUMU YA HABASHAH

1. Pamene maquraysh adazindikira za kusamuka kwa asilamu kupita ku Habashah, adatumiza anthu awiri[20] ndi mphatso kukayipempha mfumu ya Habashah kuti iwabweze omwe adasamuka mwa asilamu.

2. Chomwecho Najāshī (r.a) adakana kuwapereka pambuyo pakuti Ja`far mwana wa Abī Tālib adamufotokozera tchutchutchu wa chipembedzo cha Chisilamu, ndikuwerenga kwa Iye ndime zoyambilira za Sūrah Maryam.

3. Chomwecho awiriwo adabwerera manja-manja, ndipo Najāshī (r.a) adalandira chisilamu pamodzi ndi omwe adali naye mwa Aqissīsīina (ophunzira) ndi a Ruhbān (owopa Mulungu) munthawi imeneyo (chaka cha 7 pambuyo pa utumiki).

4. Ndipo chomwecho Allah adabvumbulutsa (mau awa); [**Ndipo uwapeza oyandikira ubwenzi ndi Asilamu, ndi awo akunena kuti: "Ife ndi Akhirisitu". Zimenezo nchifukwa chakuti mwa Iwo alipo ophunzira ndi owopa Mulungu, ndi chifukwanso Iwo (Akhiristu) sadzitukumula**].

5. Pambuyo pake adamwalira Najāshī (r.a) ndipo chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamupempherera Iye pamene Jibrīl (a.s) adamudziwitsa za kumwalira kwake. Ndipo chimenechi ndicho chiyambi cha pemphero la Janazah ya maliro omwe ali kutali.

[20] Ndipo Iwo ndi `Amr mwana wa al-`Ās ndi `Umārah mwana wa al-Walīd. Ndipo Iwo adati kwa Najāshī (r.a): "E! Inu mfumu! Ndithu alowa mdziko lanu lino anyamata ochokera mwa Ife omwe ndi opulikira. Asiya chipembedzo cha anthu awo ndipo ayambitsa chipembedzo chomwe sitikuchidziwa Ife ingakhalenso Inuyo. Ndipo atitumiza kwa Inu pankhani ya Iwo (akulu-akulu) olemekezeka a anthu awo, mwa atate a azimalume awo ndi abale awo kuti muwabwezere kwa Iwo". Chomwecho Najāshī (r.a) adati kwa Iwo: " Sindiwapereka mpakana nditawaitana ndi kuwafunsa". Chomwecho pamene adawaitana ndikuwafunsa, Ja`far (r.a) adati kwa Iye: "E! Inu mfumu! Ife tidali anthu a umbuli; kumapembedza mafano ndikumadya zofa zokha, ndikumachita zonyasa, ndikumadula ubale, ndikumachita zoipa kwa oyandikana nawo nyumba, ndipo wamphamvu wa Ife adali kudya ofowoka. Kufikira mpakana pamene adatumiza Allah kwa Ife Mtumiki ochokera mwa Ife, yemwe tikumudziwa mtundu wake ndi kuona kwake, ndi kukhulupirika kwake ndi kudzisunga kwake. Chomwecho adatiyitanira ku umodzi wa Allah ndikuti tisamuphatikize Iye ndi chinthu china, ndikuti tisiye zomwe tidali kuzipembedza mwa mafano, ndipo adatilamula kunena zowona, ndi kulumikiza ubale, ndi kukhala bwino ndi oyandikana nawo, ndi kusiya zoletsedwa komanso kukhetsa mwazi. Ndipo adatiletsa zonyasa ndi kuyankhula bodza, ndi kudya chuma chamasiye. Ndipo adatilamura za mapemphero ndi kusala chakudya ndi kupereka cha ulere ndi kuchita Hajj, chomwecho tidamukhulupirira ndi kumuvomereza".

MAFUNSO

Kodi maquraysh adachita chiani pamene adadziwa za kusamuka kwa asilamu kunka ku Habashah? Kodi Najāshī adawapereka kwa adani awo? Kodi Najāshī adalandira Chisilamu? Kodi ndi chiani chomwe chidavumbulutsidwa pankhani yokhudza Iwo? Kodi Najāshī adakhala moyo pambuyo pa zimenezi? Kodi Mtumiki (s.a.w) adapempherera maliro akutali asadamwalire Najāshī?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Maquraysh adatumiza nthumwi ziwiri kwa Najāshī kuti Iye athamangitse asilamu mdziko lake, koma Iye sadachite ndipo adalandira Chisilamu limodzi ndi omwe adali naye. Ndipo kenako adamwalira chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamupempherera Salah ya Janazah.

(29) KUTULUKA KWA MTUMIKI (S.A.W) MU KUSALIDWA (NDI KUPANIKIZIDWA)

1. Mchaka cha khumi cha utumiki adagwirizana anthu asanu mwa olemekezeka a maquraysh, chomwecho adang'amba chikalata (chija)[21].

2. Chomwecho adatuluka Mtumiki (s.a.w) limodzi ndi omwe adali naye kuchokera mu kusalidwa ndi kutsekerezedwa kuja, pambuyo pakuti adakhala kumbali kwa mapiri pafupi-fupi zaka zitatu.

3. Sichimafika kwa Iwo chilichonse cha chakudya koma mobisa basi, mpakana Iwo amadya masamba a mitengo.

4. Ndipo adali Mtumiki (s.a.w) atafotokoza kuti ndithu chiswe chadya chikalata chija, ndipo chomwecho pamene maquraysh adachitsitsa (chikalatacho) kuti aching'ambe, adachipeza chili monga momwe adafotokozera Iye.

MAFUNSO

Kodi ndi chaka chanji chomwe chidang'ambidwa chikalata chija? Ndipo adakhala zaka zingati Mtumiki (s.a.w) mukusalidwa? Kodi chidali kufika kwa Iye chilichonse chochokera mchakudya? Kodi adafotokoza za chiani asadatuluke mukusalidwaku?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka cha khumi chidang'ambidwa chikalata, chomwecho adatuluka Mtumiki (s.a.w) mukusalidwa pambuyo pa zaka zitatu.

[21] Ndipo oyambilira kuyankhula mwa Iwo adali Zuhayr chomwecho Iye adati: "Eh! Inu anthu a Makkah! Zoona Ife tizidya chakudya ndikuvala zovala pomwe ana a Hāshim ndi Muttalib akuwonongeka? Osatha kugulitsa ingakhalenso kugulidwa katundu wawo? Ndikulumbira Allah, sindikhala pansi mpakana chitang'ambidwa chikalata chopondereza ndi chodula ubalechi". Chomwecho adathandizira mau akewo anthu anai otsala. Chomwecho Abu Jahl adati: "Iyi ndi nkhani yomwe yagamulidwa usiku ndipo akambirana za iyo malo ena (osati pano)".

(30) GULU LA NTHUMWI ZA KU NAJRĀN

1. Mchaka cha khumi (10) lidabwera gulu la nthumwi la Akhirisitu a ku Najrān[22].

2. Idawafika Iwo nkhani ya Iye (s.a.w) kudzera mwa (asilamu) osamukira ku Habashah, ndipo Iwo adali anthu makumi awiri (20).

3. Chomwecho adawawerengera Iwo Mtumiki (s.a.w) Qur'ān, chomwecho adakhulupirira onse.

4. Pamenepo Abū Jahl adawazazira[23] chifukwa cha kulandira kwawo Chisilamu, chomwecho Iwo adati kwa iye: "**Zanu ndi zomwe muli pa izo, ndiponso zathu ndi zomwe ife tasankha**".

MAFUNSO

Kodi ndi ndani omwe adadza kwa Mtumiki (s.a.w) ngati nthumwi mchaka cha khumi? Kodi ndani yemwe adawawuza Iwo za Iye? Kodi adakhulupirira? Ndani yemwe adawazazira chifukwa cha Chisilamu chawo? Kodi adamuyankha ndi yankho lotani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka chimenecho zidabwera kwa Iye nthumwi mwa Akhirisitu ena a ku Najrān, chomwecho adamvetsera Qur'ān ndipo adakhulupirira.

[22] Mzinda omwe uli pakati pa Makkah ndi Yemen

[23] Iye (Abu Jahl) adati kwa Iwo: "Sitidaonepo anthu apaulendo opusa ngati Inu. Anthu anu akutumizani kuti muzadziwe nkhani ya munthu uyu (Muhammad) ndiye Inu mukusiya chipembedzo chanu?". Chomwecho Iwo adati kwa Iye: "Mtendere ukhale pa Inu, sitichita nanu za umbuli, zanu ndi zomwe muli pa izo ndipo nafe zathu ndi zomwe tasankha". Chomwecho Allah adavumbulutsa pa nkhani imenei (mau akuti): "**Amene tidawapatsa buku kale ili lisanadze, akulikhulupirira ili. Ndipo likawerengedwa kwa Iwo akuti; "Talikhulupirira, ndithu ichi nchoona chochokera kwa Mbuye wathu. Ilo lisanadze, Ife tidali ogonjera (Mulungu)". Iwo adzapatsidwa malipiro awo kawiri chifukwa chakuti amapirira ndi kuchotsa choipa pochita chabwino, ndipo mzimene tawapatsa akupereka chopereka. Ndipo akamva zopanda pake amazipewa ndipo amati: "Ife tili ndi zochita zathu, ndipo nanunso muli ndi zochita zanu, mtendere ukhale pa Inu. Ife sitifuna kutsutsana ndi mbuli**".

(31) KUMWALIRA KWA KHADIJAH (R.A) - KUKWATIRA SAWDAH NDI `ĀISHAH (R.A)

1. Mchaka cha khumi cha utumiki, adamwalira mai olemekezeka Khadījah (r.a), chomwecho adandawula Mtumiki (s.a.w) chifukwa cha Iye kudandaula kwakulu, chifukwa chakuti Iye adali kumukonda ndikuchotsa kwa Iye zosawutsa za maquraysh.

2. Chomwecho adakwatira pambuyo pake Sawdah (r.a), pambuyo pakuti mamuna wake adamwalira. Ndipo Iye adali atakhulupirira Allah ndi Mtumiki wake (s.a.w) ndipo adasiyana nawo abale ake.

3. Ndipo pambuyo pa mwezi umodzi adamanga ukwati ndi `Āishah (r.a) mwana wa Abūbakr Siddīq (r.a), Iye ali mchaka chachisanu ndi ziwiri (7) mmoyo wake.

4. Ndipo Iye sadakwatirepo namwali kupatula Iye (`Āishah), ndipo adalowana naye ku Madinah.

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe adamwalira mai olemekezeka Khadījah? Kodi ndi liti lomwe adakwatira Sawdah? Ndi liti lomwe adakwatira `Āishah? Kodi adali ndi zaka zingati panthawiyo? Kodi adakwatirapo namwali kupatula Iye? Kodi adalowana naye kuti?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo mchaka cha khumi adamwalira mai olemekeza Khadījah, chomwecho Iye adakwatira pambuyo pake Sawdah, kenako `Āishah ali ndi zaka zisanu ndi ziwiri za kubadwa. Ndipo adalowana naye ku Madinah.

(32) KUMWALIRA KWA MALUME AKE

1. Pambuyo pa kumwalira kwa mai olemekezeka Khadījah (r.a) pafupi-fupi mwezi umodzi, adamwaliranso malume ake Abū Tālib, chomwecho adandaula pa Iwo Mtumiki (s.a.w).

2. Ndipo chidatchedwa chaka chimenechi kuti; **chaka cha madandaulo**, chifukwa chakuti Iye adataya mmenemo mkazi wake ndi malume ake.

3. Ndipo adali malume ake kukhulupirira kuona kwa zomwe adadza nazo Mtumiki (s.a.w), koma kuti Iwo sadanene liwu la umboni wa chikhulupiriro (Shahādah) mpakana mphindi yomalizira ya moyo wawo, chifukwa cha kuopa kutozedwa ndi maquraysh.

4. Ndipo pa nkhani yawo adabvumbulutsidwa (mau awa): "**Ndithu Iwe sungathe kumuwongola amene ukumfuna, koma Allah amuongola yemwe wamfuna**". Chomwecho tikupempha Allah akuti awafetsere pamodzi ndi otsara onse mwa abale ake (s.a.w).

MAFUNSO

Kodi malume ake adamwalira liti? Kodi chaka chimenechi chidatchedwa kuti chiani? Kodi malume ake adali kukhulupirira za kuona kwa utumiki wake? Nchifukwa chiani sadanene mau awiri awumboni (wachikhulupiriro)?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo mchaka chimenechi adamwalira malume ake Abū Tālib, ndipo Iwo adali athandizi ake akulu-akulu. Ndipo Iwo sadalandire chisilamu chifukwa chowopa kutozedwa ndi anthu awo.

(33) KUSAWUTSA KWA MAQURAYSH PA MTUMIKI (S.A.W)

1. Pambuyo pa kumwalira kwa mkazi wa Mtumiki (s.a.w) ndi malume ake, adayamba maquraysh kumuzunza Mtumiki.

2. Chomwecho Iwo adali kumuthira mchenga ndikumayika nyasi za ziweto pa Iye ali mmapemphero ake.

3. Ndipo adamukwenya ulendo wina nati kwa Iye: “Iwe ndi amene ukufuna kuyichita milungu kukhala mulungu mmodzi yekha basi?”.

4. Chomwecho adabwera patsogolo Abūbakr (r.a) namuleletsa kwa Iwo, ndipo adati kwa Iwo: “**Zoona mukumupha munthu chifukwa cha kunena kuti Mbuye wanga ndi Allah?**”.

MAFUNSO

Kodi maquraysh adachita chiani kwa Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kumwalira kwa mkazi wake ndi malume ake? Kodi anali kumusawutsa ndi chiani? Kodi adati chiani kwa Iye pamene adamukwenya? Kodi ndani adamuleletsa kwa Iye?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adalimbikira masawutso a maquraysh pa Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kumwalira kwa mkazi wake ndi malume ake, kotero kuti adatsimikiza za kumupha.

(34) NSAMUKO WA KU TĀIF

1. Pamene adaona Mtumiki (s.aw) kumupeputsa kwa maquraysh, adasamuka mchaka cha khumi kupita ku Tāif limodzi ndi Zaid (r.a) mwana wa Hārithah.

2. Ndipo Iye adalunjika ku mtundu wa Thaqīf napempha kwa Iwo kuti amuthandizire pa anthu ake.

3. Koma Iwo adamuyankha yankho loipa ndipo adalamura zitsiru zawo ndi akapolo awo kuti amutukwane, ndipo adamulasa ndi miyala kotero kuti adayenderera magazi mmisempha ya miyendo yake.

4. Ndipo adali Zaid mwana wa Hārithah (r.a) kutchinga miyala kwa Iye, kotero kuti adavulala ndi mabala mmutu mwake[24].

5. Chomwecho pamene Iye sadapeze chabwino chilichonse kwa Iwo, adabwerera[25] ku Makkah pambuyo pakuti adakhala pakati pawo mwezi (umodzi).

[24] Chomwecho Jibrīl (a.s) adamudzera nati kwa Iye: "Ndithu Allah wandilamura kuti tikumvere (pa zomwe ungandilamure) pa anthu ako, chifukwa cha zomwe achita kwa Iwe". Chomwe Iye (s.a.w) adati kwa Iye: "E! Allah! Awongoleni anthu anga, pakuti Iwo sakudziwa (chomwe akuchita)". Chomwecho Jibrīl adati kwa Iye: "**Adanena zoona yemwe adakutcha kuti ndiwe wachifundo ndi chisoni**".

[25] Ndipo pamene Iye adafika pa Nakhlah (malo ena pafupi ndi Tāif), lidabwera kwa Iye gulu la nthumwi la majini (ziwanda) kudzamvetsera Qur'an. Ndipo Iwo ndi ochokera mwa omwe amatsatira Musa (madalitso ndi mtendere wa Allah ukhale pa Iye). Chomwecho pamene adaimva adakhala chete, ndipo adabwerera kwa anthu awo kukawachenjeza ndipo adawafikitsira nkhani ya Mtumiki (s.a.w). Ndipo Allah wafotokoza nkhani yawo mu Surah Jinn.

MAFUNSO

Ndi liti lomwe adasamuka Mtumiki (s.a.w) kupita ku Tāif? Kodi ndani adasamuka naye limodzi? Kodi adalowera kuti? Kodi Iwo adayankha pempho lake? Kodi ndani yemwe adali kumutchinjiriza? Kodi kukhala kwake pakati pawo kudali kotalika motani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adakula masautso adasamuka Mtumiki (s.a.w) kupita ku Tāif Iyeyo ndi Zaid mwana wa Hārithah. Ndipo adapereka nkhani yake kwa mtundu wa Thaqīf, chomwecho Iwo adamuyankha yankho loipa ndipo adamusawutsa. Ndipo adali Zaid kutchinjiriza kwa Iye masautso.

(35) ISRĀ' YAKE (ULENDO WAKE WA USIKU) NDI MI`RĀJ YAKE (KUKWERA KWAKE KUMWAMBA)

1. Mchaka cha khumi ndi chimodzi (11), Allah adamulemekeza Iye (s.a.w) ndi Isrā' komanso Mi`rāj.

2. Chomwecho Isrā' ndiko kulunjika kwake Mtumiki (s.a.w) usiku kuchokera ku Msikiti opatulika (ku Makkah) kupita ku Msikiti wa Aqsā (ku Jerusalemu).

3. Ndipo Mi`raj[26] ndiko kukwera kwake (s.a.w) kupita ku dziko la kumwamba, ndipo ulendo umenewu mapemphero asanu adakakamizidwa.

4. Ndipo mmawa ma usiku wa Isrā, Jibrīl (a.s) adamphunzitsa Iye mapemphero ndi nthawi zake.

MAFUNSO

Mchaka chanji chomwe Allah adamulemekeza Iye ndi Isrā komanso Mi`rāj? Kodi Isrā ndi Mi`rāj ndi chiani? Nchiani chomwe chidakakamizidwa mu ulendo umeneu? Kodi ndani yemwe adamphunzitsa Iye mapemphero ndi nthawi zake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka cha khumi ndi chimodzi (11) adamulemekeza Iye Allah ndi ulendo wa usiku ndi kukwera kumwamba. Ndipo mmenemo adakakamizidwa mapemphero asanu.

[26] Ndipo pali kusemphana maganizo pa nkhani imenei kuti; kodi (Mi`raj) idachitika ndi thupi ndi mzimu, kapena mzimu okha basi? Chomwecho gulu lochuluka la Ahlussunnah Wal Jamā`ah (anthu a Sunnah ndi gulu lolungama) lili pa fundo yakuti (Mi`raj) idachitika ndi ziwirizi limodzi (thupi ndi mzimu). Koma Aishah ndi Mu`awiyah ndi al-Hasan (Basri) amati; zidachitika ndi mzimu okha basi.

(36) KUITANIRA MAFUKO KU CHIPEMBEDZO

1. Adapitirira Mtumiki (s.a.w) kwa zaka khumi akuwaitanira maquraysh ku chipembedzo mofewa ndi modekha. Koma pamene adaona kukula kwa kudzikweza kwawo ndi kukakamira kwawo ndi kutsekereza kwawo kufalitsa chipembedzo,

2. Adatuluka mchaka cha khumi ndi chimodzi cha utumiki kupita ku mafuko munthawi za misika yawo.

3. Ndipo adayamba kuwaitanira ku chipembedzo, chomwecho ena a Iwo adali kumuyankha yankho loipa, pomwe ena amayankha yankho labwino.

4. Ndipo omwe adali oipitsitsa pa kumuyankha adali Banū Hanīfah, lomwe ndi gulu la Musaylamah onama.

MAFUNSO

Kodi ndi zaka zingati zomwe adapitirira Mtumiki (s.a.w) kuwaitanira maquraysh? Kodi ndi chaka chanji chomwe Iye adatuluka ku mafuko? Kodi Iwo adali kumuyankha ndi yankho lotani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka chimenechi adadzipereka Mtumiki (s.a.w) Iye mwini ku mafuko mmisika, ndipo ena mwa Iwo adavomera ndipo ena mwa Iwo adayankha mayankhidwe oipa.

(37) CHIYAMBI CHA CHISILAMU CHA MA ANSĀR (R.A)

1. Mchaka cha khumi ndi chimodzi (11), linabwera ku Makkah gulu la anthu asanu ndi mmodzi (6) ochokera mwa Aluya a ku Yathrib[27] kudzachita Hajj.

2. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawaitanira ku Chisilamu ndi ku kumuthandizira pa kufalitsa uthenga wa Mbuye wake.

3. Chomwecho adamukhulupirira ndi kumuvomereza, ndipo adati kwa Iye: "Tikulumbira Allah, Ndithu uyu ndiye Mneneri yemwe akumatilonjeza naye Ayuda, chomwecho asakupitirireni pa (kumulandira) Iyeyu".

4. Ndipo pamene Iwo adabwerera kumudzi kwawo, adafotokozera anthu awo nkhani ya Mtumiki (s.a.w), ndipo adawaitanira ku Chisilamu. Chomwecho idafalikira nkhani yake (s.a.w) mmizinda, ndipo ichi ndicho chiyambi cha kulandira chisilamu kwa Aluya a kuyathrib.

MAFUNSO

Kodi ndani yemwe adabwera ku Makkah mchaka cha 11 cha utumiki? Kodi adati chiani kwa Iwo Mtumiki (s.a.w)? Kodi adamukhulupirira? Nchiani chomwe adachita pambuyo pa kubwerera ku midzi yawo?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo mchaka chimenechi lidabwera ku Makkah kudzachita Hajj gulu la anthu asanu ndi mmodzi mwa Aluya a ku Madinah, chomwecho adalandira Chisilamu ndipo adafalitsa nkhani ya Mtumiki (s.a.w) ku Madinah Munawwarah.

[27] Kuchokera mu mtundu wa Khazraj

(38) MALOJEZANO A PAPHIRI OYAMBA

1. Mchaka cha khumi ndi ziwiri (12) anabwera anthu khumi ndi awiri (12)[28] mwa Aluya aku Yathrib.

2. Chomwecho Iwo adakumanizana ndi Mtumiki (s.a.w) pa nkumano wa paphiri oyambilira, ndipo adalonjezana naye[29] pa Chisilamu ndi fundo (zotsatirazi;).

3. Kuti Iwo sadzamuphatikiza Allah ndi chinthu china, ndi kuti sadzaba, Ndikuchita chiwerewere, ndikupha ana awo, ndikuti sadzanena bodza lamkunkhuniza lomwe akulipeka pakati pa manja awo andi miyendo yawo, ndikuti sadzanyozera pa chinthu chabwino. Chomwecho ngati atakwaniritsa (zimenezi) adzapeza munda wa mtendere, ndipo ngati atapalamula chilichonse muzimenezi, ndiyekuti chigamulo chawo chili kwa Allah; ngati atafuna akhululuka ndipo ngati atafuna alanga.

4. Ndipo pamene anabwerera kwawo, Mtumiki (s.a.w) adatumiza limodzi nawo oti akawaphunzitse[30] Chisilamu ndi kuwapatsa kumvetsetsa pa chipembedzo. Chomwecho chidafalikira chisilamu chifukwa cha Iwo, kotero kuti padalibe nyumba ndi imodzi yomwe mnyumba za ku Madinah koma kuti mumatchulidwa mmenemo nkhani ya Chisilamu.

MAFUNSO

Ndani yemwe adafika mchaka cha khumi ndi ziwiri? Kodi adakumanizana ndi Mtumiki? Kodi adalonjezana naye pa chinthu chanji? Kodi Mtumiki (s.a.w) adawachitira chiani pamene Iwo amabwerera?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka cha khumi ndi ziwiri adabwera anthu khumi ndi awiri kuchokera ku Madinah, chomwecho adalonjezana nawo Mtumiki (s.a.w) pa malo a paphiri. Ndipo adabwerera ndi kufalitsa chisilamu ku Madinah.

[28] Khumi ochokera mwa mtundu wa Aws, ndipo awiri ochokera mwa Khazraj.
[29] Ndipo amatchedwa malonjezano amenewa kuti “malonjezano a akazi”.
[30] Yemwe ndi Mus`ab mwana wa `Umayr ndipo adali kutchedwa kuti Muqri “Muwerengetsi/Mphunzitsi”.

(39) NKUMANO WA PAPHIRI WACHIWIRI

1. Mchaka cha khumi ndi chitatu (13) cha utumiki, lidabwera gulu la nthumwi lokwana amuna makumi asanu ndi awiri[31] ndi mphambu zitatu (73) ndi akazi awiri mwa Aluya aku Madinah.

2. Chomwecho adalonjezana naye Mtumiki (s.a.w) pa nkumano wachiwiri wa paphiri (pa fundo zakuti); amupembedze Allah ndipo asamuphatikize ndi chilichonse, ndikuti amuteteze[32] Mtumiki (s.a.w) pamene adzasamukira kwa Iwo.

3. Ndipo kenako adatulutsa akulu-akulu khumi ndi awiri mwa Iwo, ndipo chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati kwa Iwo: "Inu ndinu adindo (oyimirira) pa anthu anu pa zomwe zili mwa Iwo; (ndinu) adindo monga udindo wa ophunzira a `Īsā kwa `Īsā mwana wa Maryam (a.s), ndipo Ine ndine mndindo (oyimirira) pa anthu anga".

4. Chomwecho adabwerera ku Madinah ndipo Chisilamu chidafalikira kumeneko kuposa ulendo oyambilira.

MAFUNSO

Kodi ndi ndani omwe adafika kwa Mtumiki (s.a.w) mchaka cha 13? Kodi adalonjezana naye? Kodi adachita chiani pambuyo pa malonjezano? Kodi Mtumiki (s.a.w) adati chiani kwa adindo? Kodi Iwo adakhazikika ku Makkah?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Mchaka cha khumi ndi chitatu zinabwera kwa Mtumiki (s.a.w) nthumwi 73 zachimuna ndi akazi awiri, chomwecho zidamulonjeza Mtumiki (s.a.w) pa nkumano wachiwiri wa paphiri. Ndipo zidabwerera chomwecho zidafalitsa Chisilamu ku Madinah Munawwarah.

[31] Amuna makumi asanu ndi mmodzi ndi mphambu ziwiri (62) ochokera mu mtundu wa Khazraj, ndipo khumi ndi mmodzi (11) ochokera mu mtundu wa Aws.
[32] Amuteteze kutanthauza "amuthandize".

(40) NSAMUKO WA ASILAMU KUPITA KU MADINAH

1. Pamene adadziwa maquraysh za kufalikira kwa Chisialmu ku Madinah, adakhwimitsa chilango pa ophunzira a Mtumiki (s.a.w).

2. Chomwecho Iye adawalamula za kusamukira ku Madinah ndi kukakhala limodzi ndi abale awo ma Ansār.

3. Chomwecho adatuluka mMakkah mobisa, chifukwa cha kuopa kuti maquraysh angawatsekereze kusamuka[33].

4. Ndipo Abūbakr (r.a) adafuna kusamuka, koma Mtumiki (s.a.w) adamuletsa, chomwecho adatsalira limodzi ndi iye ku Makkah.

MAFUNSO

Kodi maquraysh adachita chiani atadziwa za kulandira Chisilamu kwa ma Ansār? Kodi Mtumiki (s.a.w) adawalamura chiani ophunzira ake? Kodi Iwo adatuluka motani? Kodi Abūbakr adasamuka nawo limodzi?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pamene adalandira chisilamu anthu aku Madinah, adawonjezera anthu aku Makkah pa kupereka masawuwtso kwa Asilamu. Chomwecho adawalamura Mtumiki (s.a.w) za kusamukira ku Madinah. Chomwecho adasamuka ena a Iwo pambuyo pa ena.

[33] Chomwecho anali kunyamuka mozemba mmodzi pambuyo pa mmodzi, kuti akakwanitse kumpembedza Allah yemwe chidasakanikirana chikondi chake ndi milofu yawo (thupi lawo) ndi magazi awo. Kotero kuti adali osalabada za kusiyana ndi midzi yawo ndi kutalikirana ndi makolo awo komanso ana awo, bola ngati zimenezo zili zosangalatsa Allah ndi Mtumiki wake (s.a.w).

(41) MGWIRIZANO WA MAQURAYSH ZA KUMUPHA MTUMIKI (S.A.W)

1. Pamene maquraysh adaona kuti Mtumiki (s.a.w) ali ndi ophunzira ndi athandizi omuteteza ndi kufalitsa kuitanira kwake, adatsimikiza za kumupha[34].

2. Ndipo adagwirizana kuti atenge kuchokera mu mtundu uliwonse mnyamata, ndikuti asonkhane (anyamatawo) patsogolo pa nyumba yake. Chomwecho akatuluka amumenye kumenya kwa munthu mmodzi.

3. Ndicholinga chakuti ufalikire mwazi wake pakati pa mitundu (yonse), chomwecho abale ake asathe kuchita nkhondo ndi Aluya onse.

4. Koma Allah adamudziwitsa Mtumiki (s.a.w) za zomwe adagwirizana maquraysh, ndipo adamulamura kuti asamukire ku Madinah.

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe adagwirizana maquraysh za kumupha Mtumiki (s.a.w)? Kodi adagwirizana pa fundo yanji? Nchifukwa chiani adagwirizana pa zimenezo? Kodi Allah adamudziwitsa Mtumiki (s.a.w)?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adatsimikiza maquraysh za kumupha Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kufalikira kwa chisilamu ndi nsamuko, chomwecho adamuchitira ndale ndipo Allah adamulamura za kusamuka.

[34] Pambuyo pa kukambirana pakati pawo, Abu Jahl adati: “Ine ndili ganizo lina sindikudziwa ngati mwalitulukira, lomwe nlakuti timuphe…..(mpakana kumapeto)”. Chomwecho onse adatsimikizira ganizo lakelo ndi kugwirizana pa zimenezo. Izi zidachitika chomwechi kuti chiyambi cha kufalikira kwa chisilamu chikhale malo ena osakhala ku Makkah ndipo ili ndilo luntha la umulungu, chifukwa chakuti chikadafalikira chisilamu ku Makkah, odana (nacho chisilamu) akadati; “Ndithu ma Quraysh adafuna ufumu wa Aluya chomwecho adatenga munthu (mmodzi) mwa Iwo ndikumulamura kuti anene kuti Iye ndi Mtumiki, kuti ingakhale njira yopezera zolinga zawo.

(42) KUSAMUKA KWA MUSTAFĀ (MTUMIKI S.A.W)

1. Adalunjika Mtumiki (s.a.w) kwa Abūbakr (r.a) ndipo adamudziwitsa za lamuro la Allah kwa Iye. Chomwecho Abūbakr adamupempha Iye za kukhala naye limodzi, ndipo Iye adati: “Inde”.

2. Ndipo kenako adakonza (ngamila) zokwera ziwiri za ulendo wawo (awiriwo) ndipo adazipereka kwa katswiri olozera njira.

3. Ndipo adamulamura kuti adzabwere nazo (zokwerazo) pambuyo pa masiku atatu ku phanga la Thawr[35].

4 Chomwecho mu usiku umene adatsimikiza za kutuluka mnyumba yake, adazungilira anyamata a maquraysh nyumba, uku Mtumiki (s.a.w) ali mkati mwake.

5. Ndipo pamene idafika nthawi ya kutuluka, adalamura Mtumiki (s.a.w) mwana wa malume ake `Alī (r.a) kuti agone pa kama lake ndi cholinga chakuti asakaike aliyense za kupezeka[36] kwake mnyumba yakeyo. Ndiponso adamulamura Iye kuti abweze zosungitsidwa[37] za anthu kwa eni ake.

6. Ndipo kenako adatuluka pamaso pa adani ake[38], chomwecho Allah adaika tulo pa Iwo kotero kuti aliyense sadamuone Iye. Ndipo kenako adakakumanizana ndi Abūbakr nayenda awiriwo mpaka adakafika ku phanga la Thawr ndikubisala mmenemo.

---

[35] Kenako Mtumiki adasiyana naye Abubakr ndipo adapangana naye kuti akakumane kunja kwa Makkah.

[36] Chifukwa chakuti ma Quraysh adali kubwereza-bwereza kuyang’ana kuchokera mmipata ya chitseko kuti adziwe kupezeka kwa Mtumiki (s.a.w).

[37] Chifukwa chakuti aliyense pa Makkah yemwe adali ndi chinthu chomwe amachiwopera adali kuchiyika kwa Iye.

[38] Uku Iye akuwerenga mau awa; ﴿**Ndipo tawayikira chotsekereza patsogolo pawo ndi chotsekereza pambuyo pawo, chomwecho maso awo tawaphimba tero Iwo saona**﴾.

MAFUNSO

Kodi adalunjika kuti Mtumiki (s.a.w) pambuyo pakuti adalamulidwa za kusamuka? Kodi adachita chiani awiriwo pambuyo pa zimenezo? Kodi adamulamura chiani otsogolera njira? Kodi ndi usiku uti omwe adazungulira anyamata a ma Quraysh nyumba yake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adagwirizana Mtumiki (s.a.w) ndi Abubakr za kusamuka ndipo adakonza zokwera ziwiri. Ndipo adatuluka Mtumiki (s.a.w) mnyumba yake, ndipo Iwo sadamuone mpaka adakafika Iye ndi nzake ku phanga la Thawr ndi kubisala mmenemo.

(43) KUFUFUZA KWA MAQURAYSH MTUMIKI (S.A.W)

1. Pamene adadzuka maquraysh usiku umenewo ndipo sadapeze aliyense mnyumba ya Mtumiki (s.a.w) koma mwana wa malume ake `Alī, udakula zedi mkwiyo wawo.

2. Chomwecho adatumiza anyamata awo ndi malupanga ndi dondo kuti akamufufuze Mtumiki (s.a.w) mbali zonse.

3. Ndipo adakonza kwa amene angawabweretsere kapena kuwalozera Iye ngamira zana limodzi (100) ngati mphotho.

4. Ndipo ndithu adafika – mukufufuza kwawo – pa phangalo kotero kuti mmodzi wa Iwo akadayang'ana mkatimo akadamuona Mtumiki (s.a.w) ndi nzakeyo.

5. Ndipo Abūbakr adawaona Iwo ndipo adalira. Chomwecho Mtumiki adati kwa Iye: "**Usadandaule, ndithu Allah ali nafe**". Chomwecho Allah adaika khungu mmaso mwa maquraysh ndipo adabwerera manja-manja.

MAFUNSO

Kodi maquraysh adachita chiani mmawa wa usiku umenewo? Kodi adatumiza aliyense kukafufuza za Iye? Kodi adakhazikitsa chiani ngati mphotho ya zimenezo? Kodi adafika mpakana kuti pa kumufufuza Iye? Kodi ndani yemwe adawaona Iwo mphangamo?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo mmawa maquraysh adawafufuza (awiriwo) ndipo adafika pa phangalo koma Iwo sadawatulukire (awiriwo). Ndipo Abūbakr adawawona chomwecho adalira. Ndipo kenako (maquraysh) adakonza ngamira zana limodzi kukhala mphotho kwa yemwe angawalozere za Iye.

(44) KUTULUKA KWA MTUMIKI (S.A.W) KUPHANGA

1. Pambuyo pakutha kwa kumufufuza Mtumiki (s.a.w), Iye adatuluka limodzi ndi bwenzi lake. Ndipo adakhala mphangamo masiku atatu.

2. Ndipo `Abdullāh (r.a)[39] mwana wa Abūbakr adali kuwadzera madzulo ndi kuwafotokozera nkhani za maquraysh.

3. Ndipo adali mlongo wake – Asmā' (r.a) – kuwabweretsera chakudya mobisa, kuwopera maquraysh.

4. Ndipo pamene adawadzera olozera njira uja ndi zokwera ziwiri zija mmawa wa tsiku lachitatu, Iwo adakwera ndi kuyenda kulunjika ku Madinah Munawwarah.

5. Ndipo adawafikira Iwo mnjiramo Surāqah[40], ndipo adafuna kumupha Mtumiki (s.a.w) koma adalephera.

MAFUNSO

Kodi adakhala masiku angati Mtumiki (s.a.w) ndi bwenzi lake ku phanga? Kodi ndani anali kuwabweretsera nkhani? Nanga ndani amawabweretsera chakudya? Kodi adayenda liti kupita ku Madinah? Ndani yemwe adawafikira awiriwo mnjira?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adatuluka awiriwo ku phanga pambuyo pa masiku atatu, ndipo linali banja la Abūbakr (r.a) kubwera kwa Iwo ndi chakudya ndi nkhani, ndipo kenako adayenda limodzi ndi olozera njira. Ndipo adatuluka kuwalondola Iwo Surāqh mwana wa Mālik, koma adabwerera manja-manja.

---

[39] Ndipo Iye kumamuchela ali ku Makkah kukhala ngati adagona komweko, chomwecho akamva kwa ma Quraysh nkhani ina yake yokhudzana ndi Mtumiki (s.a.w) ndi bwenzi lake, amabwera nayo usiku ndikuwafotokozera nagona kwa Iwo.

[40] Ndipo Iye adali atamva za photho yomwe adaikonza ma Quraysh kwa yemwe angawabweretsere Muhammad (s.a.w), chomwecho adamufikira Mtumiki (s.a.w) mpakana adamuyandikira. Chomwecho idapunthwa hatchi yake ndipo adagwa. Kenako adaikweranso ndikuyenda mpakana adayamba kumva kuwerenga kwa Mtumiki (s.a.w) uku Iye asakutembenuka, chomwecho miyendo ya hatchi ya Suraqah idatitimira ndipo adagwa. Kenaka adaikalipira mpakana idadzuka ndipo isadamalize kutulutsa miyendo yake lidatuluka fumbi lalikulu kukwera kumwamba kukhala ngati utsi, chomwecho Suraqah adadziwa kuti ntchito yapita pachabe ndipo adadziopera. Chomwecho adawaitana ndikuwapempha chitetezo, chomwecho adamupatsa chitetezocho, ndipo Iye adabwerera manja-manja.

(45) KUTULA PA QUBĀ' - MASJID YOYAMBA KUMANGIDWA MCHISILAMU

1. Adafika Mtumiki (s.a.w) ku Qubā' pa 2 mmwezi wa Rabī`ul Awwal, mogwirizana ndi pa 30 Septembala chaka cha 622[41] chachikunja.

2. Pambuyo pakuti adakhala zaka khumi ndi zitatu (13) mopanikizika ku Makkah, ali otsekerezedwa kusamuka ndi kuitanira (ku chipembedzo).

3. Ndipo Iye adakhala pa Qubā' masiku makumi awiri ndi mphambu ziwiri (22) pakati pa ophunzira ake ma Muhājirūn (osamuka) ndi ma Ansār (athandizi), ali otetezeka ndi okhazikika.

4. Ndipo ndithu Iye adamanga mnthawi imeneyi – Masjid ya Qubā', yomwe wayisimba Allah kuti Iyo (ndi): "**Masjid yomwe idakhazikitsidwa ndi cholinga chomuopa Allah**".

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe adafika Mtumiki (s.a.w) ku Qubā'? Kodi ndi zaka zingati zomwe adakhala ku Makkah? Kodi adakhala masiku angati ku Qubā'? Kodi adachita chiani munthawi imeneyi?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Pa 2 mmwezi wa Rabī`ul Awwal adafika awiriwo ku Qubā' mwamtendere, ndipo adakhala kumeneko masiku makumi awiri ndi mmphambu ziwiri (22). Ndipo adamanga Mtumiki (s.a.w) mkati mwa nthawi imeneyi – Masjid ya Qubā' (**Masjid yomwe idakhazikitsidwa ndi cholinga chowopa Allah**).

[41] Ndipo ichi ndipo chiyambi cha mbiri yatsopano ya kuwonekera kwa Chisilamu pambuyo pa nsamuko. Chomwecho kupyolera munsamuko umeneu chidakwaniritsidwa kwa Mtumiki (s.a.w) chikhalidwe cha abale ake mwa Aneneri (a.s) omwe adalipo Iye asadabwere. Pakuti palibe Mneneri aliyense koma kuti adanyozedwa ndi anthu ake ndipo adasawutsidwa ndi kuzunzidwa, mpakana adakakamizika kusamuka mdziko lake; kuyambira Ibrahim (a.s) mpaka Isa (a.s).

(46) KUFIKA KU MADINAH – JUMU`AH YOYAMBA MCHISILAMU – KHUTBAH OYAMBA MCHISILAMU

1. Ndipo pamene adatuluka Mtumiki (s.a.w) kuchokera ku Qubā' kulunjika ku Madinah, adamuzungulira Iye ma Ansār uku Iwo atapachikira malupanga awo, akusangalala ndi chimwemwe.

2. Ndipo idamupeza Jumu`ah ali mnjira, chomwecho adaipemphera limodzi ndi omwe adali naye mwa asilamu. Ndipo imenei ndi Jumu`ah yoyambilira komanso Khutbah wake ndi Khutbah oyambilira mchisilamu.

3. Ndipo anthu a ku Madinah adatuluka kukakumana naye (kukamuchingamira) uku ali ndi azimai ndi ana ndi adzakazi akunena kuti:

"Waonekera mwezi owala kwa Ife"

"Kuchokera ku chigwa cha Wadā`"

"Kwakakamizika kuthokoza kwa Ife"

"Nthawi zonse pamene ayitanira kwa Allah Oyitanira"

"Eh! Iwe amene watumizidwa kwa Ife!

" Wadza ndi lamuro lotsatidwa"

MAFUNSO

Ndani omwe adamuzungulira Mtumiki (s.a.w) pamene amatuluka ku Qubā'? Ndikuti komwe idamupeza Jumu`ah? Kodi adapemphera Jumu`ah ina patsogolo pake? Ndani omwe adatuluka kukamuchingamira?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Ndipo adatuluka Mtumiki (s.a.w) mmenemo uku mmbali mwake muli ma Ansār ndi ma Muhājirun, atalunjika ku Madinah. Ndipo adapemphera Jumu`ah ndi kuchita Khutbah mnjira. Ndipo adamuchingamira Iye ma Ansār kuchingamira kwakulu zedi.

(47) KULOWA KWA MTUMIKI (S.A.W) KU MADINAH – KUTULA KWAKE – CHIKONDI CHA MA ANSĀR KWA A MUHĀJIRŪN – UBALE WACHISILAMU

1. Pamene adalowa Mtumiki (s.a.w) ku Madinah, sanali kudutsa nyumba iliyonse mnyumba za ma Ansār koma kuti adali kumupempha kuti afikire kwa Iwo[42].

2. Chomwecho Iye adafikira kwa Abū Ayyūb Ansārī (r.a) mchipinda chapansi kuti zikhale zofewa kwa odzamuzonda[43].

3. Ndipo ma Ansār adali kuwakonda omwe adasamukira kwa Iwo, ndipo adali kuwatsogoza kusiya Iwo eni, kotero kuti adalimbanirana pa kofikira kwawo, chomwecho adapanga mayere kukhala choweruzira pakati pawo. Chomwecho palibe osamuka aliyense yemwe adafikira kwa Ansārī koma kudzera mkuchita mayere basi.

4. Ndipo kenako Mtumiki (s.a.w) adakhazikitsa ubale pakati pawo, ubale wachisilamu umene udayanjanitsa mitima yawo ndikuyichita kukhala ngati chinthu chimodzi[44].

MAFUNSO

Kodi adali bwanji malowedwe a Mtumiki (s.a.w) ku Madinah? Kodi adafikira kuti? Kodi adali bwanji ma Ansār ndi ma Muhājirūn? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani pakati pawo?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adafikira Mtumiki (s.a.w) kwa Abī Ayyūb Ansārī (r.a), ndipo adakhazikitsa (s.a.w) ubale pakati pa ma Muhājirūn ndi ma Ansār.

---

[42] Ndipo adali kugwira chingwe cha ngamila, chomwecho Iye (s.a.w) amanena kwa Iwo: "Isiyeni pakuti Iyo ndi yolamulidwa". Ndipo idapitirirabe kuyenda mpakana idakagwada pa khomo la Abi Ayyub Ansari (r.a).

[43] Komabe sadakondwere Abu Ayyub Ansari ndi zimenezi chifukwa cha kumulemekeza Mtumiki (s.a.w). Ndipo adali kumunyengererabe (Mtumiki s.a.w) mpakana adasuntha kupita chipinda chammwamba.

[44] Ndipo udapitirirabe ubale umenewu mpakana pamene Allah Oyera ndi Wapamwamba-mwamba adabvumbulutsa: "**Koma achibale chakubadwana, ndi amene ali oyenera (kulowerana mmalo pachuma), (zimenezi ndi zomwe zili) m'buku la Allah….**"

(48) KUSAMUKA KWA AKUBANJA – KULETSEDWA KWA ANTHU OFOWOKA – CHIYAMBI CHA QUNŪT – NTHENDA YA KU MADINAH

1. Pamene adakhazikika Mtumiki (s.a.w) ku Madinah, adatumiza uthenga kuwaitanitsa omwe adatsalira mwa akubanja ake. Chomwecho adatuluka nawo `Abdullāh mwana wa Abūbakr (r.a).

2. Ndipo adaletsa ma Mushrikūn aku Makkah ena ofowoketsedwa kuchita ulendo, ndipo adawalanga ndi chilango chopweteka.

3. Chomwecho adali Mtumiki (s.a.w) kuwachitira Duwa mu Witr ya salah ya Ishā' ndi Salah ya Subh pambuyo pa kuwerama (ruku`) komanso asadawelame[45]. Ndipo ichi ndicho chiyambi cha Qunūt.

4. Ndipo idawagwira ambiri mwa ma Muhājirīn nthenda (yotentha thupi)[46], chomwecho Mtumiki (s.a.w) adapempha Mbuye wake kuti ayichotse, chomwecho Allah adayankha pempho lake.

MAFUNSO

Kodi nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kukhazikika ku Madinah? Kodi ma Mushrikūn aku Makkah adawatsekereza asilamu onse za kusamuka? Kodi ndi nthawi yanji yomwe adali kuwapemphera Duwa Mtumiki (s.a.w)? Nchiani chomwe chidawagwira ma Muhājirīn ku Madinah?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE

Adatumiza Mtumiki (s.a.w) (uthenga) kuyitanitsa omwe adatsalira mwa akubanja lake, chomwecho adadza limodzi ndi `Abdullāh mwana wa Abūbakr (r.a). Ndipo ma Mushrikūn adawatsekereza ofowoka kusamuka, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adali kuwapemphera Duwa, ndipo ichi ndicho chiyambi cha Qunūt mu Salāh.

[45] Ichi ndicho chifukwa cha kusemphana kwa atsogoleri (a maphunziro pa Deen) pa nkhani ya malo ochitira Qunut.
[46] Chifukwa chakuti mphepo ya ku Madinah siidali kugwirizana nawo kumayambiliro.

CHIDULE CHA GAWO LACHIWIRI (LOFUNIKA KULOWEZA)

Pamene adafika zaka makumi anai (40) mmoyo wake (s.a.w), Allah adamutumiza Iye kukhala chisomo kwa zolengedwa zonse. Ndipo ndithu chinayamba chibvumbulutso ndi maloto abwino, ndipo adatsika kwa Iye Jibrīl (a.s) Iye akupembedza ku phanga la Hirā'. Ndipo adamphunzitsa momwe angawongolere anthu ku njira yolungama. Chomwecho Iye adayamba ndi kuyitanira mobisa, ndipo yemwe adali oyambilira kumukhulupirira adali mai olemekezeka Khadījah (r.a), ndi Abūbakr (r.a) ndi `Ali (r.a) ndi Zaid (r.a) mwana wa Hārithah.

Ndipo pambuyo pa zaka zitatu adalamulidwa za kuwonetsera poyera, chomwecho adawasonkhanitsa anthu ake ndi kuwachenjeza za chilango cha tsiku lomaliza.

Ndipo pamene adatsika mau ake (Allah) wapamwamba-mwamba akuti: "**Ndipo achenjeze abale ako oyandikira**", Iye adasonkhanitsa banja lake ndi abale ake ndipo adawafikitsira uthenga wa Mbuye wake. Chomwecho Abū Lahab adamuyankha kuyankha koipa.

Ndipo adali Aluya – patangotsala pang'ono kutumizikdwa kwake – kupembedza mafano ndikumapha ana awo ndi kukwilira ana awo akazi. Ndipo adali kumenya ena a Iwo makosi a ena (kuphana) pa zifukwa zing'ono-zing'ono. Chomwecho pamene adawaitanira Mtumiki (s.a.w) ku kupembedza Allah yekha basi, ndi kusiya zomwe Iwo amazitsata, adakwiya ndipo kumukonda kwawo kudasintha kusanduka udani, komanso kumuvomereza kwawo kudasanduka kutsutsa.

Ndipo pamene Iye adanyoza milungu yawo ndi kuwasimba makolo awo kuti ndi osokera, adayenda kupita kwa malume ake koyamba ndi kachiwiri ndi kachitatu. Ndipo nthawi iliyonse adali kuwayankha mwaubwino.

Ndipo ndithu adamupempha Iye malume ake pambuyo pa kubwera kwawo komaliza, kuti awasiye (ndi milungu yawo), koma Mtumiki (s.a.w) adakana ndipo adakhazikika pa kufalitsa chipembedzo uku malume ake akumuteteza.

Chomwecho pamene maquraysh adaona zimenezi kwa Iye, adayamba kumusawutsa Mtumiki (s.a.w) ndi kumuchita chipongwe. Ndipo Iye adali kuwabwezera ndi kufatsa ndi kupilira ndi kukhululuka. Ndipo kenako kusawutsa kudayendelera kwa ophunzira ake ndipo chomwecho mtundu uliwonse udayamba kulanga omwe alandira chisilamu mwa Iwo ndi chilango chachikulu zedi. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawalamura za kusamukira ku Habashah, ndipo chomwecho adasamuka (amuna) khumi mwa ophunzira ake

ndi akazi asanu, koma anabwelera pambuyo pa miyezi itatu. Ndipo umenewu ndiwo nsamuko oyambilira mchisilamu.

Ndipo ndithu adalandira chisilamu munthawi imenei Hamzah, malume a Mtumiki (s.a.w), ndi `Umar mwana wa Khattāb (r.a). Ndipo mchaka cha chisanu ndi chiwiri (7) cha utumiki, maquraysh adamusala (ndi kumutsekereza) Iye pamodzi ndi akubanja ake. Ndipo adagwirizana za kuwadula ubale kapena ampereke Muhammad (s.a.w) kuti amuphe. Ndipo adalemba zimenezi pa chikalata ndi kuchipachika pa Ka`bah.

Ndipo pambuyo pa kulowa kwa Mtumiki (s.aw) mukusalidwaku, adawalamura ophunzira ake za kusamukira ku Habashah, chomwecho adasamuka amuna makumi atatu kudza mmphambu zitatu (33) ndi akazi khumi ndi mmodzi (11).

Ndipo mchaka cha khumi cha utumiki, amuna ena ochokera mwa maquraysh adagwira ntchito yong'amba chikalata chija. Chomwecho chidang'ambidwa ndipo Mtumiki (s.a.w) adatululuka limodzi ndi omwe adali naye mu kusalidwako, pambuyo pakuti adakwanitsa zaka zitatu (3) ali kumbali kwa mapiri, popanda kufika kwa iwo chakudya koma mobisa basi.

Ndipo mchaka chimenechi linabwera gulu la nthumwi mwa Akhirisitu a ku Najrān, ndipo adalandira chisilamu. Ndipo mchaka chimenechi adamwalira mai olemekezeka Khadījah (r.a) ndi malume ake Abū Tālib. Ndipo Iye adakwatira Sawdah (r.a) ndi kulowana naye, ndipo adamanga banja ndi `Āishah (r.a) ndipo sadalowane naye.

Ndipo pambuyo pa kumwalira kwa malume ake masawutso adawonjezereka, chomwecho Iye adasamukira ku Tāif ndipo adawulinga mtundu wa Thaqīf. Chomwecho adakhala pakati pawo mwezi umodzi akuwaitanira. Chomwecho sadamulandire ndipo adamusawutsa ndi kumugenda ndi miyala, chomwecho adabwerera ku Makkah.

Ndipo mchaka cha khumi ndi chimodzi Allah adamulemekeza ndi Isrā komanso Mi`rāj ndipo mmenemo adakakamizidwa mapemphero asanu. Ndipo mchaka chomwechi adayamba kutuluka ku mitundu ndi kuyiyitanira ku chisilamu, chomwecho adamukhulupirira Iye asanu ndi mmodzi mwa Aluya a ku Madinah.

Mchaka cha khumi ndi zitatu (13) kuchokera mu utumiki, lidabwera gulu la amuna 73 ndi azimai awiri mwa Aluya a ku Madinah, chomwecho adamukhulupirira ndikubwerera ku Madinah, ndipo chomwecho kudawonjezekera kufalikira kwa Chisilamu.

Ndipo mchaka chimenechi adalamura ophunzira ake za kusamukira ku Madinah. Ndipo pamene zimenezi zidawafika maquraysh adatsimikiza za kumupha Mtumiki (s.a.w), chomwecho Allah adamulamura Iye za kusamuka.

Ndipo adazungulira maquraysh nyumba yake usiku wa kusamuka kwake, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatuluka pamaso pawo pambuyo pakuti Allah adaika tulo pa iwo. Ndipo adayenda limodzi ndi Abūbakr Siddīq (r.a) kupita ku phanga la Thawr nabisala mmenemo masiku atatu. Ndipo kenako adayenda awiririwo tsiku lachitatu mpakana adafika ku Qubā' tsiku lachiwiri mmwezi wa Rabī`ul Awwal. Chomwecho adakhala (s.a.w) ku Qubā' masiku 22, omwe mkati-kati mwake adamanga Masjid ya Qubā'.

Ndipo kenako adasuntha kupita ku Madinah ndipo Jumu`ah idamupeza mnjira, chomwecho adayipemphera ndipo imenei ndi Jumu`ah yoyambilira komanso Khutbah wake ndi Khutbah oyambilira mchisilamu.

Pamene Iye (s.a.w) adatulukira mbali ya ku Madinah anthu adatuluka kukakumana naye ali osangalala ndi kufika kwake.

Ndipo Iye adafikira kwa Abī Ayyūb Ansārī (r.a), ndipo pamene adakhazikika adatumiza uthenga kuitana omwe adatsalira mwa akubanja ake. Chomwecho Iwo adafika limodzi ndi `Abdullāh mwana wa Abūbakr (r.a). Ndipo ma Mushrikūn adaletsa ena mwa ofowoka kusamuka, ndipo Mtumiki (s.a.w) anali kuwapephera zabwino, ndipo chimenechi ndicho chiyambi cha Qunūt.

ZAMKATIMU

MUTU	TSAMBA
Gawo loyamba	03
Bwana athu Muhammad (s.a.w)	03
Mndandanda wa makolo ake ndi kumwalira kwa atate ake	04
Kubadwa kwake ndi kuyamwitsidwa kwake	05
Kumwalira kwa mai ake ndi kuyang'aniridwa kwake	06
kuleledwa kwake ndi kumwalira kwa agogo ake	07
Kuweta kwake nkhosa ndi ulendo wake oyamba ku Shām	08
Ulendo wake wachiwiri kupita ku Shām	09
Ukwati wake ndi mai olemekezeka Khadījah	10
Kuweruza kwake pakati pa maquraysh za kuika mwala wakuda	11
Kukula kwake (s.a.w)	12
Moyo wake patangotsala pang'ono kulandira utumiki	13
Kufotokoza mwachidule gawo loyamba	14
Gawo lachiwiri – Kuyamba kwa chivumbulutso	15
Kakhalidwe ka Aluya chisadafike chisilamu	16
Kuyitanira mobisa	17
Oyambilira wa okhulupirira	18
Kuyitanira mowonetsera	19
Kusonkhanitsa kwake abale ake	20
Kusonkhana kwa maquraysh polimbana ndi Mtumiki (s.a.w)	21
Kubwera kwa ma quraysh kachiwiri	22
Kubwera kwa maquraysh kachitatu	23
Kupereka mazunzo kwa maquraysh pa Mtumiki (s.a.w)	24
Kupereka mazunzo kwa maquraysh pa ma Sahābah (r.a)	25

Zofuna za maquraysh kwa Mtumiki (s.a.w)	26
Nsamuko oyamba wa ku Habashah	27
Kulandira chisilamu kwa Hamzah ndi `Umar	28
Kusalidwa kwa Mtumiki (s.a.w)	29
Nsamuko wachiwiri wa ku Habashah	30
Kulandira chisilamu kwa mfumu ya Habashah	31
Kutuluka kwa Mtumiki (s.a.w) mukusalidwa	33
Nthumwi za ku Najrān	34
Kumwalira kwa Khadījah – Kukwatira Sawdah ndi Aishah (r.a)	35
Kuwalira kwa malume ake	36
Kusawuwutsa kwa maquraysh pa Mtumiki (s.a.w)	37
Nsamuko wa ku Tāif	38
Isrā' yake (s.a.w) ndi Mi`rāj yake	39
Kuitanira mafuko ku chipembedzo	40
Chiyambi cha chisilamu cha ma Ansār	41
Malonjezano oyamba apaphiri (`Aqabah)	42
Nkumano wachiwiri wapaphiri	43
Nsamuko wa Asilamu kupita ku Madinah	44
Kugwirizana kwa maquraysh za kumupha Mtumiki (s.a.w)	45
Kusamuka kwa Mustafā (Mtumiki s.a.w)	46
Kufufuza kwa maquraysh Mtumiki (s.a.w)	48
Kutuluka kwa Mtumiki (s.a.w) ku phanga	49
Kutula (kufika) pa Qubā' – Masjid yoyamba mchisilamu	50
Kufika ku Madinah – Jumu`ah yoyamba mchisilamu	51
Kulowa kwa Mtumiki (s.a.w) mMadinah	52
Kutula kwake	52
Chikondi cha ma Ansār pa ma Muhājirūn	52

Kusamuka kwa akubanja 53

Kuletsedwa kwa ofowoka 53

Chiyambi cha Qunūt 53

Nthenda ya ku Madinah 53

Chidule cha gawo lachiwiri (lofunika kuloweza) 54